3110
File




Graham Ingram

*Baptist Publishing House*

OF THE BAPTIST MISSION OF ZAMBIA
P.O.BOX 1995 LUSAKA

# Kuitana kwa Mulungu

Graham Ingram

## ZA MKATIMU

Phunziro — Tsamba

MAU OYAMBA .......... 1

MUTU

1 KUITANIDWA KWA NOWA NDI MULUNGU .......... 3

2 KUITANIDWA KWA ABRAHAMU NDI MULUNGU .......... 8

3 KUITANIDWA KWA MOSE NDI MULUNGU .......... 13

4. KUITANIDWA KWA ARONI NDI MULUNGU .......... 19

5 KUITANIDWA KWA YOSWA NDI MULUNGU .......... 23

6 KUITANIDWA KWA ELISA NDI MULUNGU .......... 28

7 KUITANIDWA KWA YESEYA NDI MULUNGU .......... 33

8 KUITANIDWA KWA YEREMIYA NDI MULUNGU .......... 37

9 KUITANIDWA KWA PETRO NDI MULUNGU .......... 42

10 KUITANIDWA KWA ANDREYA NDI MULUNGU .......... 47

11 KUITANIDWA KWA YAKOBO NDI YOHANE NDI MULUNGU .......... 51

12 KUITANIDWA KWA PAULO NDI MULUNGU .......... 56

13 KUITANA KWA MULUNGU KWA KWA INUYO .......... 61

Bvuto lathu lalikuru ndi kusalola kwathu kuti timvere kuitana kwa Mulungu. Monga momwe phula m'makutu athu limatipangitsa kuti tisamanva bwino zomwe anthu ali kulankhula, cotero kusalola ndi kusamvera kwathu kumatipanga ife kukhala osamva kuitana kwa Mulungu. Ngati mitima yathu iri yolola tidzamva kuitana kwa Mulungu nthawi zonse.

MAFUNSO:

1. Kodi cifuniro ca Mulungu pa moyo wanga ndi ciani?

2. Kodi timawiringula bwanji posamvera kuitana kwa Mulungu?

3. Kodi Mkristu wosamvera angakhale Mkristu wokondwa?

m'miyoyo yathu. Koma monga momwe galasi la dothi limaononga kuwala cotero ucimo womwe uli kwa ine umafafaniza masomphenya a Yesu.

4. KUITANA KWA KWA INUYO

Kuitana kwa Mulungu kuli kuitana kwa pamwamba ndi konita patsogolo. Monga Aisrayeli mu cipululu sitinafike ke Dziko Lalonjezano. Pali zambiri zakuti tidzicite ndi zambiri zakuti tiphunzire tisadafikeko. Aliyense wa ife ali nayo mbali yakuti acite. Funso sindilo lakuti "kodi Mulungu ali kundiitana ine?" koma "kodi andiitana kuti ndikacitenji?" 1 Akorinto 12:4-11 anena momveka kuti Mulungu amapatsa mphatso zosiyanasiyana kwa ciwalo ciri conse ca mu mpingo wace, koma mphatso zonsezi nzakuti zigwinitsidwe nchito yace. Mulungu ali ndi colinga ca moyo uli wonse wa Mkristu. Nchito yathu ifeyo ndiyo yakupeza kuti colingaci ndi citi ndipo tikatero ticicite.

Kodi timapeza bwanji cifuniro cace ca Mulungu ca pa ife? Mulungu amalankhula nafe ndi kuitiitana mu njira zosiyana zambiri.

A. Kupyolera m'Mau ace. Ici ndiyo njira yopambana koposa. Ingakhale pomwe tiri kuwerenga Buku Lopatulika lathu mwa mtseri, kapena pomwe timva Mau ali kulalikidwa pamene Mulungu adzalankhula nafe.

B. Kupyolera mwa pemphero pamene tiri kulingirira Mau a Mulungu.

C. Kupyolera mwa abwenzi a Cikristu. Mulungu pena anganene nafe kupyolera mwa mbusa, mdikoni kapena umboni wa abwenzi a Cikristu ena.

D. Kupyolera mu zinthu zina. Mulungu pena amatsogolera miyoyo yathu mu njira zine zakuti cifuniro cace ca pa ife cimakhala coonekeratu.



## MAU OYAMBA

Munthu wina ananena kuti timangofika pena pace pomwe tifuna m'moyo wa Cikristu. Ngati izi ziri zoona ndiyekutino Akristu ambiri nga mtima wa theka m'zofuna zao zakuti apite patsogolo mu zinthu za Mulungu.

Tsiku lina ndinapita ku cipatala ku wodi lobalira azimai kukaona ka mwana komwe kadangobadwa mwa tsopano. Monga ana ena ali onse kanali kamwana kosangalala. Wodi lonselo linadzala ndi ana okhaokha, kulira kolimba kuonetsa kuti tinali ta mphamvu. Ndi zinthu zomwe anthu ambiri amakondwera kudziona. Koma ngati ndingapite ku malo amodzimodziwo patapita miezi isanu ndi umodzi ndipo ndikukaona ana omwe aja ali cimodzimodzi monga analiri poyamba paja ndi ngadere nkhawa kwambiri. Cifukwatu ana sanapangidwe kuti adzingokhala ana. Iwo ngakuti adzikula kukhala anyamata ndi atsikana amphamvu, ndipo tsiku lina kudzakula kukhala amuna ndi akazi.

Komatu izi ndizo zomwe timadziona kawirikawiri m'mipingo ya Cikristu. Anthu omwe amayembekezedwa kuti akule kukhala athanzi ndi amphamvu mu Cikristu amangokhalabe ana mu za uzimu. Mlembi wa Ahebri alankhula za Akristu m'masiku amenewo pomwe anthu anali otero. Iye akuti, "Pakuti mungakhale mwayenera kukhala aphunzitsi cifukwa ca nyengoyi, muli nako kusowanso kuti wina aphunzitse inu zoyamba za ciyambidwe ca maneno a Mulungu; ndipo mukhala monga ofuna mkaka, osati cakudya cotafuna. Pakuti yense wakudya mkaka alibe cizolowezi ca mau a cilungamo; pakuti ali khanda."(Ahebri 5:12-13).

Colinga ca maphunzirowa ncakuti Akristu acoke mu maleledwe ndi kulowa mu nyumba yogwiriramo ncito. Moyo wa Cikristu sumathera paciyambi! Izi nzoonatu. Mulungu ali ndi nzeru ndi colinga ca moyo wathu. Mitu imeneyi ndiya kuti ithandize munthu wina ali yense wowerenga kuti aturukire colinga cimeneci.

Cakudya comwe Mkiristu amakulirapo ndico Mau a Mulungu. Cotsogolera miyoyo yathu ya Cikristu ndico Mau a Mulungu. Cotero mitu yotsatirayi ndi, Maphunziro a M'Buku Lopatulika. Mituyi njakuti idziwerengedwa pamodzi ndimBuku Lopatulika, kumaona malemba a m'Buku Lopatulika omwe aperekedwa. Ngati satero ndiyekutitu sidzidzathandiza konse ndipo ndikokuti ndidzalephera mu zomwe ndinaganira kuti zicitike.

Pemphero langa nilakuti maphunziro a menewa adzakuthandizani inu ndi kukudyetsani inu kufikira kumapeto "Kuti munthu wa Mulungu akhale woyenera, wokonzeka kucita nchito iri yonse ya-bwino." (2 Timoteo 3:17).



Paulo anena Akristu aku Roma kuti anali "oitanidwa a Yesu Kristu." (Aroma 1:6). Mu 1 Akorinto anena za kulalikira Uthenga Wabwino kwa Ayuda ndi Ahelene. Kwa anthu ambiri cinaoneka ngati cinthu copusa, kwa anthu ena cinali cosafunika konse koma "kwaiwo amene ali oitanidwa......Kristu mphamvu ya Mulungu ndi cidziwitso ca Mulungu." (1 Akorinto 1:2-24). Onse amamva kunja kwa kuitana kwa Uthenga Wabwino koma ena okha omwe amamva kuitana kwa mzimu mkati ndi kuulandira Uthenga Wabwinowo. Kodi inuyo muli Pati?

3. KUITANA KWA KUKHALA OFANANA NDI YESU

Kuitana kwa Mulungu koitanira cipulumutso ndi kuitana kwa kukhala moyo woyenera nthawi zonse. Buku Lopatulika linena momveka kuti simungakhale Akristu oona ndikupitiriza kumakhala monga momwe munaliri kukhalira kale. (Yakobo 2:14-17).

Akristu onse ali kuitanidwa kuti akhale oyera. (1 Akorinto 1:2). Oyera ndiwo anthu omwe "apatulidwa kukhala a Mulungu." Paulo apempha kuti "Mulungu wathu akuyeseni inu oyenera kuitanidwa kwanu, nakwaniritse comkomera conse......kuti dzina la Ambuye wathu Yesu Lilemekezedwe mwa inu."(2 Atesalonika 1:11-12).

Pali kakolasi komwe kamati,

"Kuti ukoma wa Yesu uonekere mwa inu,
Zonse zodabwitsa zace ndi za cifundo
zace ndi ungwito wace.
Inu Mzimu woyera, konzani mtima wanga.
Kufikira ukoma wa Yesu uonekere mwa
ine."

Colinga ca Mulungu ndikukupangani INU kukhala monga Yesu. (Aroma 8:29). Mulungu akonda mwana wace kopambana kotero kuti afuna dziko lonse lapansi lidzale ndi anthu ofanafana naye. Mulungu amaika Kristu m'mitima mwathu kotero kuti, monga momwe kuwala kumaunikira kuyolera mu galasi, iye awale kupyolera

anenera, kunka mu Ufumu wa Mwana wace wokondedwa. (Akolose 1:13). Kuitanaku kumadza mu njira za mbiri.

1. KUITANA KWA UTHENGA WABWINO

Mu 2 Atesalonika 2:14, kunena za umboni wa Cikristu wa Akristu omwe anali kuwalembera, Paulo akuti "Kumene anaitanako inu mwa Uthenga Wabwino wathu."

Lamulo lotsiriza la Yesu la ku mpingo wace linali lakulalikira Uthenga Wabwino ndi kupanga ophunzira. (Mateyu 28:19-20). Uthenga womwe ulalikidwa ndi anthu a Mulungu ndi kuitana kwa Mulungu kwa anthu ocimwe, kuwaitana iwo kuti acoke kumacimo ao ndi kukhala naco cikhulupiriro mwa Kristu.

Tiona kuti mukumvera lamulo la Kristu, Petro analalikira Uthenga kwa anthu amu Yerusalemu ndikuwaitana iwo kuti alape ndi kuti abatizidwe kuti macimo awo akhululukidwe, (Macitidwe 2:38).

2. KUITANA KWA MZIMU

Anthu ambiri amamva kuitana kwa Uthenga Wabwino, koma sionse amene amaulandira. Penatu, ngati muli Akristu, mudamva Uthenga Wabwino kwa nthawi zambiri kale musadadze kwa Kristu. Poyamba mudamvatu ndi makutu anu okha, komano tsiku lina mudaumva ndi mtima wanu.'

Uthenga Wabwino wolalikidwa kupyolera mwa anthu umamveka m'makutu mwathu, koma Mzimu Woyera amagwiritsa nchito mau amenewo naitana m'mitima yathu.

Yesu analankhula kwa khamu lalikuru la anthu nati, "Palibe mmodzi akhoza kudza kwa Ine koma ngati Atate wondituma Ine amkoka iye. ....." (Yohane 6:44). Ife tingaumve Uthenga Wabwino koma Mulungu yekha, pogwira nchito mwa Mzimu Woyera, ndiye angatipangitse kulakalaka kudza kwa Kristu.



MUTU 1

## KUITANIDWA KWA NOWA NDI MULUNGU

LEMBA: Genesis 6.

VESI LOLOWEZA: *".....Nowa anali munthu wolungama ndi wangwiro m'mibadwo yace; Nowa anayendabe ndi Mulungu."* *Genesis 6:9.*

Nthawi zina Mulungu amaitana anthu kuti amucitire umboni mu nthawi zoipisitsa ndi zobvuta. Nowa anaitanidwa ndi Mulungu mu nthawi yotereyi.

1. CIYAMBI CA KUITANIDWA KWACE

Tiphunzira mu Genesisi mutu wa 3 kuti munthu anaukira Mulungu nagwa m'macimo. Kuyambira pomwepo kunka mtsogolo anthu onse 'anagwa', monga momwe tinenera. Paulo atiuza kuti anthu "Onse anacimwa naperewera pa ulemerero wa Mulungu." (Aroma 3:23).

Kuma mu mbadwo uli wonse Mulungu anali ndi anthu aceace, opulumutsidwa ndi cisomo, kukhala mboni zace. M'masiku a Nowa ucimo unali waukuru koposa ndikuti unali ponseponse kotero kuti anthu asanu ndi atatu okha anapulumutsidwa pamene Mulungu anaweruza dziko ndi cigumula. Werengani 1 Petro 3:20.

Ucimo unalowa koposa kotero kuti Mulungu analengeza kuti adzaweruza dziko cifukwa ca macimo awo. (Genesis 6:5-7 ndi 11-12).

2. NOWA ANALI WOLUNGAMA PAMASO PA MULUNGU

Mulungu asadaitane munthu kuti am'tumikire, amayamba wamuitanira ku cipulumutso. "Tidapulumutsidwa kuti tikatumikire' komatu sitingatumikire kufikira titapulumutsidwa. Zonse zomwe tingayese kuti timutumikire

Mulungu pamene sitinapulumutsidwe ziri zopanda pace ndi zosalandiridwa kwa iye. Nowa anali wapulumutsidwa kale pamene Mulungu anamuitana cifukwa tiwerenga mu Genesisi 6:8-9:

"Koma Nowa anapeza ufulu pamaso pa Yehova"
"Nowa anali munthu wolungama"
"Ndi Wangwiro m'mibadwo yace"
"Nowa anayendabe ndi Mulungu"

Nowa anakhulupirira malonjezano a Mulungu. Iye anayendabe mtsogolo m'cikhulupiriro kufikira tsiku lomwe Mulungu anati adzatuma Mpulumutsi. Genesis 3:15 muli lonjezano limeneli ngakhale siliri vesi lofewa kulimvetsa. Nowa anapulumutsidwa kupyolera mwa cikhulupiriro. Iye anali naco cilungamo monga mphatso yacokera kwa Mulungu, monga momwe tingakhalire nayo.

3. MULUNGU ANAITANA NOWA KUTI AKHALE MLALIKI WA CILUNGAMO

Mu Petro Waciwiri 2:5 Petro amchula Nowa kuti 'wamthenga wa cilungano.' Wa mthenga ndi yemwe pena amaliza lipenga, longa lomwe lioneka pa cikutulo ca buku lathuli, kapena yemwe amakweza mau ace, kuti munthu ali yense akhoza kumva. Yohane Mbatizi anali wa mthenga. Iye anapfuula ndi mau akuru kuti Yesu anali 'Mwana wa Nkhoza wa Mulungu.'

Nowa anaitanidwa kuti akhale wa mthenga. Iye anaitanidwa kuti anene momveka ndi mopfuula za ucimo wamu mbadwo wacewo. Iye anaitana anthu kuti alape ndi kutembenuka kucoka ku macimo awo.

Ici ndi cinthu colimba ndi cobvuta kucicita. Ambiri a aneneri amu Cipangano Cakale anali 'amithenga a cilungamo' ndipo iwowa anali kuponyedwa miyala kufikila kufa cifukwa ca uthengawo. Pamene Yesu analilira macimo a Yerusalemu anati, "Yerusalemu, Yerusalemu, iwe wakupha aneneri ndi wakuponya miyala iwo atumidwa kwa iwe!" (Luka 13:34). Yesu anali



MUTU 13

## KUITANA KWA MULUNGU KWA INUYO

LEMBA: 1 Akorinto 12:4-11.

VESI LOLOWEZA: *"Kukatero tikupempherer aninso nthawi zonse, kuti Mulungu wathu akuyeseni inu oyera kuitanidwa kwanu........"*
*2 Atesalokika 1:11.*

Buku Lopatulika liri ndi zambiri zonena za kuitana kwa Mulungu. Taona zitsanzo za kuitana kwa Mulungu kwa anthu ena omwe anakhala m'masiku pamene Buku Lopatukikali linali kulembedwa. Izi zipangatu nthano zokondweretsa kwambiri; koma ici sicinali cifukwa cace cakuti zilembedwe. Mu Aroma 14:4 Paulo alemba tere:

*"Pakuti zonse zimene zinalembedwa kale zinalembedwa kutilangiza kuti mwa cipiriro ndi citonthozo ca malembo, tikhale ndi ciyembekezo."*

Buku Lopatulika ndi buku lomwe liri loona. Timvamo mau a Mulungu akutiuza ife zomwe iye afuna kuti tidziwe kuti tikhale anthu monga momwe iye afunira kuti tikhalire.

Monga mwana wolowerera tonsefe tasocera kucoka kwa Mulungu kunka kumaiko akutari. (Luka 15:13). Buku Lopatulika likuti cifukwa ca ucimo wathu takhala alendo ndi anthu akumaiko ena pamaso pa Mulungu. (Aefeso 2:12). Dziko lakutari ndi dziko la cilendo. M'Cipangano ca Kale tiwerenga momwe ana a Israyeli adakhalira akopolo mu dziko lacilendo, Aigupto. Limodzi la maphunziro athu ndi phunziro la Mose yemwe Mulungu adamutuma kukawaitana kuti aturuke mu dziko limeneli, ndi kuwatsogolera iwo ku Dziko Lalonjezano la Kanani. Ici ndico cithunzi ca colinga cace ca Mulungu ca kwa ife tonse. Iye afuna kutiitana kucoka ku dziko la alendo la ucimo, ulamuliro wa mdima monga momwe

ndico mkhalidwe wa Mulungu umene atikonda nawo natipatsa ife cipulumutso cace ngakhale ife sitiri oyenera, ndipo monga Saulo, takhala otsutsana naye. Koma cisomo cimaticepetsa ife poyamba cisadatipulumutse. Saulo wonyanda uja unadzicepetsadi ndithu, koma pamene anaceptsedwa Mulungu adaululira kwa Yesu monga Mpulumutsi wace kucoka ku ucimo. (Agalatiya 1:6, Macitidwe 9:17-18).

M'mene anthu ena amanenera ndi kucitira tingaganize kuti ici cinali cimariziro ca nzeru ya Mulungu. Paulo akuti Mulungu "anakondwera mwa iye kuti adabvumbulutsa mwana wace mwa ine KUTI NDIKALALIKIRE IYE KWA AMITUNDU." (Agalatiya 1:16). Hananiya, wophunzira wokhulupirika yemwe anatumidwa kudzamulangiza zacikhulupiriro ca Cikristu, anauzidwa kuti, "Pita pakuti iye ndiye cotengera canga cosankhika conyamula dzina langa kwa Amitundu ndi mafumu, ndi ana a Israyeli." (Maciridwe 9:15).

Sipadapita nthawi yaitari paja pomwe Saulo adapulumutsidwa kuti aitanidwe ku utumiki. Saulo wocimwa uja anasandulika Paulo Mtumwi. Tiberenga kuti "Ndipo anakhala pamodzi ndi akuphunzira aku Damasiko masiku ena. Ndipo pomwepo m'masunagoge anamlalikira Yesu......." (Macitidwe 9:19-20).

Palibe umboni monga umboni watsopano, Mkristu monga Mkristu watsopano, palibe citsanzo koposa citsanzo ca wocimwa wotembenuka watsopano yemwe ali wodzadzidwa ndi Mzimu Woyera. Musayembekeza kuitana kwina kwa mtsogolo, Khalani abwino opambana a Mulungu monga mungathere, TSOPANO LINO.

MAFUNSO:

1. Kodi ndi maphunziro ndi mphatso zotani zomwe Mulungu wakupasani? Kodi ali kundiganizira zotani za moyo wanga?
2. Kodi ndakhala waphindu kotani kwa Mulungu kuyambira paja ndidatembenuka?
3. Kodi ndi cifukwa ciani tiribe munthu wina wonga Paulo mu Zambia?



mlaliki wamkuru koposa wa cilungamo ndipo anampacika iye.

Ici cakhala ciri cotero kwa anthu omwe analalikira cilungamo. M'modzi wa Akristu akuru mu Africa anali munthu wa ku Uganda wocedwa dzina lace Blasio Kigozi. Iyeyu anali akali wa cinyamata pamene anafa koma m'masiku amoyo wace wa ufupiwu, anagwiritsidwa ncito ndi Mulungu kuti anthu ambiri adze kwa Kristu ndi kudzetsa citsitsimutso ca uzimu mu mpingo. Blasio analakira kuti anthu atembenuke kucoka ku macimo awo ngati iwo anali kufuna kudziwa madalitso a Mulungu. Iye ananena kuti kusiyana kokha kwa Akristu ndi akunja mu dziko la Uganda kunali kwakuti akunja anali kucimwa poyera, pamene Akristu anali kucimwa mwa mtseri. Ndipo anthu sanali kufuna kumamva zinthu zamtundu woterewo kotero kuti Blasio anakomana ndi mtsutso wa ukuru. Iye anadziwa mwambi wakuti, "Iye amene amatsogolera kukayamba Nyalugwe (Kaingo) ndiye amene amapwetekedwa nakhala ndi zironda.

Tisanamvesetse ncito yobvuta yotereyi tiyenera kutsimikiza ainthu zina zowerengeka.

a. Tiyenera kutsimikiza kuti macimo athu anakhululukidwa.

b. Tiyenera kutsimikiza kuti tiri kukhala moyo wa Cikristu tsiku liri lonse, kulapa tsiku ndi tsiku macimo athu, Mau a Mulungu atilonjeza ife, "Koma ngati tiyenda m'kuunika, monga Iye ali m'kuunika, tiyanjana wina mnzace, ndipo mwazi wa Yesu Mwana wace utisambitsa kuticotsera ucimo wonse." (1 Yohane 1:7).

c. Tiyenera kutsimikiza kuti tikondadi woci mwa yemwe tiri kumulalikira cilungumayo.

## 4. NOWA ANAITANIDWA KUCITA CINTHU CACIKURU CA CIKHULUPIRIRO

Ulaliki wa Nowa sunapambane konse iai;

anthu asanu ndi awiri pambali pa iye mwini, anapulumutsidwa! Kupambana nthawi zonse sindiwo muyeso wa kukhulupirika iai, ngakhale tiri kufuna kukopa ambiri kuti adze kwa Ambuye.

Ngakhale anthu anakana kumvera mthenga wa Mulungu, panalibe kobvuta pakati pa iye ndi uthenga wacewo. Cobvuta cinali kuuma kwa mitima yao. Paulo ananena kwa Akorinto, "Koma ngatinso Uthenga Wabwino wathu uphimbika, uphimbika mwa iwo akutayika; mwa amene Mulungu wa nthawi yino ya pansi pano unacititsa khungu maganizo ao a osakhulupirira, kuti ciwalitsiro ca Uthenga Wabwino wa ulemerero wa Kristu, amene ali cithunzithunzi ca Mulungu, cisawawalire." (2 Akorinto 4:3-4).

Cotero Mulungu anaweruza dziko lapansi ndi cigumula cacikuru momwe anthu onse kusiya asanu ndi atatu okha omwe anapulumuka koma onse anaonongeka. Kuti asanu ndi atatu aja apulumuke Nowa analamulidwa ndi Mulungu kuti amange cingalawa ca mitengo cocedwa combo. Werengani Genesis 6:13-18.

Mulungu anamulamuliranso kuti acimange kukhala cacikuru cokwanira kunyamula nyama ndi mbalame, Kotero kuti moyo udzayambenso mu dziko la tsopano pamene cigumula cidzapita. (Genesis 6:19-21).

Cinalidi cingalawatu cacikuru ndithu. Ziganizidwa kuti cinali cingalawa comwe cinali mapazi 450 utari wace ndi mapazi 75 mbwambi mwace. Cinali ndi madenga atatu ndipo utali wace kunka m'mwamba unali mapazi 45. Nowa anayenera kucimanga combocitu pamene kunalibe ngakhale cizindikiro ca mvula. Iye anayemera kumvera Mulungu monga mwa ma Mau ace; mvera Mulungu mu cikhulupiriro. Mosakaika anthu anali kumuseka iye, koma Nowa adacimangaa comboco. (Genesis 6:22).

Kodi tomamumvera Mulungu pamene ali kulankhula nafe ngakhale ifeyo sitidziwa momwe zingacitikire?



ndi zofunika. Mlimi wa ulesi ndi woipa, kapena mai wa mbanja, kapena mwana wa skulu, sadzakhala mbusa wolimbika gugwira nchito, mdikoni kapena mdikoni wacikazi kapena Mpunzitsi wa Sande skulu wolimbika.

2. BVUTO LA MULUNGU

Saulo anali munthu yemwe analandira cikonzekero coposa kwambiri, komatu pena pace anali kulakwa. Tonsefe tidabadwa mu dziko lapansili ndi cinthu cimodzi cacikuru mu cilengadwe, ucimo. Mulungu pena angatikozetsere ife kuti tikhale moyo woyenera koma ici sicitanthauza kuti ife tifuna kukhala moyo woyenera wace ai. Ponena zoona mitima yathu ndi yomwe yakhala motsutsana ndi Mulungu.

Saulo poyamba anacita ndi mphamvu zace zonse kutsatsana nayo nchito ya Mulungu. Iye anathandizra pakupha mmodzi wa Akristu abwino koposa yemwe sanakhalenso, Stefano. (Macitidwe 7:58-8:1). Iye anacita zonse zomwe akadakhoza kuthetsa Cikristu. (Macitidwe 9:1-2, 22:4-5). Iye ananena za iye mwini kuti anali wamkuru wa ocimwa onse. (Timoteo 1:15).

3. KUITANA KWA MULUNGU

Mulungu anapanga nzeru zace cifukwa ca ucimo, Mulungu afuna kutipanganso ife atsopano poyamba, pamene sanayambe kucititsa nzeru yace nchito. Sicokwanira kwa ife kukhala okhulupirika, a cangu kapena acipembedzo. Saulotu zonsezi anali nazo asadakhale Mkristu.

Pa njira ya ku Damasiko Mulungu adamtembenuza iye mu njira yocitisa cidwi koposa. (Macitidwe 9:3-4). Mfarisi wonyanda, yemwe anali wodzikhulupirira yekha ndi zomwe anali kucita, anacititsidwa khungu ndipo anatsogoleredwa pomugwira dzanja lace monga kamwana kakang'ono. (Macitidwe 9:8).

Paulo adati ndi cisomo ca Mulungu comwe cidamuitana iye. (Agalatiya 1:15). Cisomo

mu bweya wambuziwu. (Macitidwe 18:3). Masiku atsogolo mwacemo, monga wotumidwa(m'mishonare), anatha kucita nchito yotereyi ndi kumapeza ndarama zogulira cakudya. Mulungu adalamulira kuti alaliki ndi a mishonare ayenera kumalipiridwa ndi anthu a Mulungu. (Timoyeo 5:17-18, 1 Akorinto 9:14). Ena a adani a Paulo, anali kumanena kuti iye anali kulalikira uthenga kuti apeze cuma. Ndipo cifukwa ca ici iye anasankha kumalalikira kopanda malipiro ndipo ndikumapeza cakudya cace pa nchito ya kupanga mahema. (1 Akorinto 9:3-4, 6-7 ndi 18). Anthu a Mulungu pena angakhale osakoma mtima, nthawi zina, kwa abusa awo. Iwo amakhala mokoma ndi mosangalala naganiza kuti mbusa ayenera kumakhala mosiyana nawo. Ndi cinthu cabwino, kuti munthu aliyense amene afuna kukhala mlaliki azidziwa nchito ya manja yomwe angamapezerepo cakudya cace ngati nkoyenera.

E. Iye analandira maphunziro opambana kwambiri. Pamene anali mnyamata anapita ku Yerusalemu komwe anakaphunzira pansi pa mphunzitsi wamkuru Gamalieli. (Macitidwe 22:3).

Ifenso tiyenera kulandira maphunziro opambana omwe tingakhoze kulandira. Mulungu akhoza kutigwiritsa nchito ngakhale tiri maphunziro ocepa kwambiri, monga momwe tidainera kwa Petro, komatu Mkristu wodzipereka ndi wamaphunziro abwino ali wopambana Mkristu wodzipereka koma yemwe ali wosaphunzira kwambiri. Tifuna Akristu ophunzira kotero kuti iwo akhoza kucitira umboni ndi kuphunzitsa omwe sali Akristu.

Saulo anali cotengera comwe cinali cokonzedwa bwino, pamene Mulungu adamuitana iye. Ngati ukali wa cinyamata ndipo Mulungu sadakuululire nchito ya moyo wace kwa iwe, sizitanthauza kuti zinthu zomwe muli kucita tsopanoli ziribe kanthu ai. Phunzirani zinthu zonse zimene mungakhoze ndi kudziwa zonse zomwe mungathe mu zinthu zomwe ziri zabwino



5. NOWA ANAPULUMUTSIDWA M'CIWERUZIRO
Werengani Genesis 7:6-16,23.

Buku Lopatulika liphunzitsa kuti combo ndi cafaniziro ca cipulumutso pa tsiku lomariza la ciweruziro. Werengani 1 Petro 3:20-21 ndi 2 Petro 3:5-7.

Tiphunziranso:

a. kuti m'masiku otsiriza anthu adzanyozera. 2 Petro 3:4.

b. kuti kudzakhala macimo ambiri ndi cikhulupiriro cocepa. Mateyu 24:10-13.

c. kuti okhawo omwe adzakhala ali mu combo ca Mulungu ndiwo adzapulumutsidwe. Comboci ndi mpingo, banja la Mulungu. Lomwe tilowamo kupyolera mwa cikhulupiriro. Nowa anamanga combo mwa cikhulupiriro. Iye ndi banja lace linalowamo mwa cikhulupiriro.

MAFUNSO:

1. Kodi tiri 'angwiro' mu mbadwo wathu; kapena firi kugawana nao macimo ace?

2. Kodi tiri kumacenjeza anthu ngakhale ali kumatiseka?

3. Kodi tiri mu combo ca Mulungu?

4. Kodi tiri kumvera kuitana kwa Mulungu monga momwe Nowa adacitira?

MUTU 2

## KUITANIDWA KWA ABRAHAMU NDI MULUNGU

LEMBA: Genesis 12:1-5, 15:1-6, 16:1-6, 17:1-8, 21:1-3, 22:1-14.

VESI LOLOWEZA: *"Ndi cikhulupiriro Abrahamu, poitanidwa, anamvera kuturuka kunka ku malo amene adzalandira ngati colowa........"* *Ahebri 11:8.*

Ngati Nowa aima ngati munthu wolungama mu m'badwo woipa, Abrahamu aima ngati munthu wa cikhulupiriro cacikuru m'masiku omwe kunalibe Buku Lopatulika, nyumba yopempherera, ndi ena owerengeka okhulupirira kuti amlimbikitse cikhulupiriro cace.

Baku Lopatulika limasulira cikhulupiriro kuti ndi 'cikhazikitso ca zinthu zosayembekezeka, ciyesero ca zinthu zosapenyeka." (Ahebri 11:1). Cikhulupiriro ndiko kukhulupirira zomwe mwe Mulungu anena ndipo pomwepo kumacita momwemo. Bwenzi wanga angandiuze kuti ali dilaiva wabwino ndipo ndinganene kuti ndimkhulupirira. Koma ngati sindiri wolola kukwera mu galimoto lace ndi kukhulupirira moyo wanga m'manja ace, mau anga ali mau opanda kunthu. Ndiribe cikhulupiriro ndi zomwe bwenzi langa uja andiuza.

1. KUMVERA KUITANA KWA MULUNGU

Mulungu anapanga lonjezano ndi Abrahamu.

*"Ndipo ndidzakuyesa iwe mtundu wa ukuru, ndipo ndidzakudalitsa iwe, ndi kubukitsa dzina lako; nakhale iwe mdalitsa."* *(Genesis 12:2).*

Koma lonjezanoli lisanakwanitsidwa iye anayenera kumvera kuitana kwa Mulungu.



Mulungu adakonzeratu njira. Ife nchito yathu ndiyo yakupeza njirayi ndipono nkumayendamo.

M'moyo woyambirira wa Saulo munali zinthu zambiri zomwe zidamkonzera iye nchito yace ya mtsogolo.

A. Iye adabadwira mu mzinda waukuru, Tariso, komwe iye adakapeza maphunziro abwino ndi mkhalidwe. (Macitidwe 11:39). Ici cidadzamkhalira bwino pomalankhula ndi mafumu ndi anthu a nzeru m'masiku a mtsogolo. (Macitidwe 26:2 ndi Macitidwe 17:17-18).

B. Iye anabadwa mwana wa mbadwa ya Ciroma. Makolo ace anali ayuda, koma atate wace anakhala mbadwa ya Ciroma. (Macitidwe 22:25-26). Uwu unali penatu mwai cabe womwe Wolamulira adampatsa iyeyu cifukwa ca nchito yomwe iye adacita kwa wolamulirayu. Ici cikadakhala cimodzimodzi ngati munthu yemwe sali mbadwa ya muno mu Zambia akadapatsidwa mwai wakukhala mbadwa ya mu Zambia ndi a President cifukwe ca nchito zabwino zomwe munthuyu wadzicita mu dziko lino.

Ici cidaoneka kuti cinali camtengo wapatari ndi copindulitsi mu nchito ya Paulo. Mbadwa za Ciroma zanali kupatsidwa citetezo comwe sicidapatsidwa kwa anthu ena wamba.

C. Iye adakula monga M'yuda. (Afilipi 3:5). Ici citanthauza kuti iye adadziwa Cipangano Cakale conse kwambiri. Citanthauzanso kuti iye anatha kulalikira Yesu kwa Ayuda. (Macitidwe 9:20,22).

D. Iyeyu adaphunsitsidwanso nchito yomwe idakhala copindulitsa ku nthawi za mtsogolo za moyo wace. Mwana ali yense wa mwamuna wa Ciyuda anayenera kuphunzira nchito yamanja. Ndipo mzinda wa Tariso unali wodziwika kwambiri monga malo komwe kunali kupangidwa nsaru kucokera mu ubweya wa mbuzi. Ndipo Paulo anaphunzitsidwa kupanga mahema kucokera

MUTU 12

## KUITANIDWA KWA PAULO NDI MULUNGU

LEMBA: Macitidwe 9:1-22.

VESI LOLOWEZA: *"Koma Ambuye anati kwa iye, Pita; pakuti iye ndiye cotengera canga cosankhika, cakunyamula dzina langa pamaso pa amitundu ndi mafumu ndi ana a Israyeli." Macitidwe 9:15.*

Kuyambira kale nthawi ndi nthawi Mulungu amaitana odziwika kwambiri kuti amtsatire iye. Ndipo kuitanidwa kwawo kocokera kwa Mulungu kumadziwika ndi munthu aliyense ndipo anthu aunyinji amapindula mukuitana koteroko. Saulo wa ku Tariso anali mmodzi wa anthu otererwa. Iyeyu amacedwa kuti ndiye ali m'mishonare wamkuru koposa ena onse.

1. CIKONZETSERO CA MULUNGU

Mu kalata wa ku Agalatiya, Paulo, pofotokoza za kutembenuka kwa iye mwini akuti;

> *"Koma pamene padakomdweretsa Mulungu, amene anandipatula ndisanabadwe, nandiitana ine mwa cisomo cace, kuti abvumbulutse Mwana wace mwa.....ine." (Agalatiya 1:15-16).*

Nzeru ya Mulungu ya Saulo sidayambira pa njira ya ku Damasiko. Idayamba pomwe Mulungu analenga dziko lapansi. Nzeru za Mulungu nzodabwitsa koposa kotero kuti Iye amadziwa kali konse kuyambira paciyambi. Iye ali nayo nzeru ya miyoyo yathu yonse. Mu Aefeso 2:10 Paulo anena kuti:

> *"Pakuti ife ndife cipango cace, olengedwa mwa Kristu Yesu, kucita nchito zabwino, zimene Mulungu anazipangiratu, kuti tikayende m'menemo."*



> *"Ndipo Yehova anati kwa Abramu, Turuka iwe m'dziko lako, ndi kwa abale ako, ndi ku nyumba ya atate ako, kunka ku dziko limene ndidzakusonyeza iwe.'" (Genesis 12:1).*

Cinali cinthu cacikuru kwambiri comwe Abramu anafunsidwa kuti acicite. Iye anali kukhala ku malo ocedwa. Uri wa kwa Akaldayo. Anakhala malo omwe lero lino apanga mbali ya dziko la Iraq, cifupi ndi Peresi. Mulungu anamuuza kuti asiye mtundu wace, asiye banja lace ndi kupita ku dziko la alendo. Mulungu sanamuuze konse kuti nkuti komwe anali kupitako kufikira pomwe iye anali paulendo wopita kumaloko. Iye anali kuyenda ulendo wapafupi mitunda cikwi cimodzi kunka ku dziko lomwe linali kucedwa Kenani, lomwe lero lino lipanga mbali ya dziko la Israeli. Zinalitu monga momwe mungauuziridwe kuti mucoke kwanu ndikudzipeza nokha kuti muli ku mbali zina za dziko la Africa, Aeitopia kapena Nigeria, komwe simuli kum'dziwa minthu wina ali yense, ndiponse kulibe wina yemwe angalankhule cinenero canu. Kwa Abrahamu cinali cobvuta kwambiri cifukwa m'masiku amenewo anthu sanali kuyenda monga momwe aliri kuyendera lero ai. Ngakhale kuyenda ulendo wa mitunda mazana awiri kapena atatu cinali cinthu comwe cinali kucitika kuti basi nkufatu uku.

Mulungu anali ndi colinga cacikuru kwa Abrahamu mu Kanani. Iye akadzakhala atate wa mtundu wa tsopano. Israeli, womwe udzakhala wosankhidwira wapadera wa Mulungu. Kucokera mwa Israeli, Mpulumutsi Yesu Kristu, adzabadwamo. Kupyolera mwa Kristu anthu miyandamiyanda adzakhala nawo moyo wosatha.

Ngati Mulungu akadakufunsani inu kuti mupite ku malo akutari kukakhala mboni yace mukadapitako kodi? Mwai wa kulandira Uthenga Nabwino utipatsa ife ncito ya kuulandira. M'mishonare ali yense ayenera kucoka ku dziko la kwawo ndi kupita ku dziko la cilendo. Mulungu ali kufuna amishonare kucokera m'mitundi

## 2. UKURU WACE WA CIKHULUPIRIRO CACE

Pamene Abrahamu ananyamuka ulendo wace wa kupita ku dziko lomwe adamulonjeza anali wa zaka makumi asanu ndi awiri mphambu zisanu 75. Mulungu anamulonjeza kuti adzakhala atate wa mtundu wonse watsopano, ndipo mitundu ya mbiri idzaturuka m'menemo. Koma pa msinkhu wa zaka 75 Abrahamu nkuti analibe mwana! Sara mkazi wace anali wouma. Kukhulupirira Mulungu mu zinthu monga zimenezi munthu ayenera kukhala naco cikhulupiriro caciku ndithu.

Cikhulupiriro ca Abrahamu sicinali cocateketseka. Koposa kawiri konse cidalephera. Werengani Genesis 15:2-3. Koma Mulungu anapatsanso lonjezano lace, vesi 4-5. Cifukwa cakuti Abrahamu anakhulupirira cinthu colimba cotereci Buku Lopatulika litiuza kuti Mulungu anamucha iye kuti "cilungamo." (vesi 6). Abrahamu anapulumutsidwa mwa cikhulupiriro monga momwe ife tipulumutsidwira.

Cifukwa cakuti Abrahamu, monga ife, sanali wa ngwiro anafooketsedwanso. Iye anamvera ku zakukaika za mkazi wace ndipo anabala mwana mwa mkazi wina. (Genesis 16:1-4). Ucimo wace unacititsa kusakondwa kopambana.(16:5-6). Mulungu ali ndi njira yaceyace yakucita zinthu ndipo iye amadzicita mu nthawi ya iye mwini. Sitiyenera kumacita njira zolakwika kuti ticite zolinga zace za Mulungu.

Mulungu anali wacifundo ndipo analonjezanso lonjezano lace mwa tsopano kwa Abrahamu nthawi zambiri. Iye salephera ngakhale ifeyo timacita zosayenera kwa iye. Iye nthawi zonse ali wolola kutilandira pamene tidza kwa iye pamene tiri ndi cisoni. Werengani Genesis 17:1-8, 18:1-2, ndi 9-14.

Abrahamu anayembekeza kwa nthawi ya itari koma Mulungu anali wokhulupirika ku lonjezano lace. (Genesis 21:1-3).



(Macitidwe 12:2). Ziribe kanthu kaya timtumikira Kristu kumwamba kapena pa dziko lino lapansi malinga ngati ife timtumikira komwe Iye afuna ife kuti timtumikire.

MAFUNSO:

1. Kodi ndimaononga ana anga powapanga kukhala olakalaka zinthu zosayenera?

2. Kodi zolephera zanga zazikuru ndi ziti? Nanga ndingatani nazo?

3. Kodi Akristu adaitanidwa kudzazunzikira Kristu mu Zambia muno? Ngati ndi tero nanga ndi mu njira zotani?

(vesi 6,7,9), komatu iwowa adaleka zonsezi, pamodzi ndi ngalawa zawo zamtengo wapatari ndi makhoka awo, kumtsatira Yesu! Kodi inuyo mukadacita zoterezi? Icitu ndico cofenika comwe Yesu amacita kwa ophunzira onse. Yesu adati "Ngati munthu afuna kudza pambuyo panga, adzikanize yekha, nanyamule mtanda wace, nanditsate Ine. Pakuti yense wakufuna kupulumutsa moyo wace adzautaya; ndipo yense wakutaya moyo wace cifukwa ca Ine, ndi cifukwa ca Uthenga Wabwino, adzaupulumutsa." (Marko 8: 34-35). Yesutu sanena kuti tiyenera kusiya zonse zimene tiri nazo kuti timtsatire Iye ai, koma kuti tidzikhala olola kusiya zonse zimene zingaime njira mwathu kuti tisamtsatira ndi mtima wonse. Cingatanthauze kuti tidzasiya zinthu zomwe anthu ena aganiza kuti ziri zabwino. Ngati ufuna kukhala mlaliki uyeneratu kukhala pena wosowa kuposa momwe mukadakhalira ngati munali kucita zinchito zina. A mishonare amasiya mabanja ao, mabwenzi ao ndi dziko la kwawo lomwe alikonda koposa. Akristu onse amataya mwai wakumati nthawi yanga, talente langa, ndi ndarama zanga. Taitanidwa tonse ku 'kudzikaniza' tokha cifukwa ca Uthenga. Mipingo yina ya Cikristu iri ndi 'milungu yakudzikaniza' pomwe otsatira awo ayembekezedwa kuti adzikanize okha kanthu kena kotero kuti akhoza kupereka ndarama zambiri kuthandiza anthu ena. Yesu apereka citsanzo cakuti mlungu uli wonse kwa Mkristu uli 'mlungu wakudzikaniza.

Mumavesi omwe tangowerengawa Yesu anana kuti tiyenera kukhala olola kutaya miyoyo yathu cifukwa ca Uthenga Wabwino. Mwa abale Yakobo ndi Yohane tiona Yesu ali kuitana anthu ku mazunzo osiyanasiyana. Yohane anakhala moyo zaka zambiri kufikira anakalamba kwambiri koma anazunzikira cikhulupiriro cace. M'buku lotsiriza la Buku Lopatulika, lomwe iye adalilemba, tiuzidwa kuti iyeyu adamangidwa mundende pa cisi ca Patimo cifukwa ca umboni wace. (Cibvumbulutso 1:9). Yakobo mbali yina, anafa mnyamata. Iyeyu anafa imfa ya amaritiri m'dzanja la mfumu Herode.



Cikhulupiriro cace cinayenera kupitanso mu kuyesedwa koposa kwambiri. Kodi cikondi ca Abrahamu cokonda Mulungu cinali coposa ca mwana wace yemwe anamuyembekezera kwa zaka zambirimbiri? Mulungu anamuyesa iye pomufunsa kuti ampereke nsembe Isake. (Genesis 22:1-2). Mulungu nthawi yonseyi anali kudziwa kuti codzapezeka. (22:10-14). Kodi Abrahamu anali ndi cikhulupiriro kodi ca kukhulupirira Mulungu kucita cinthu coyenera?

Mu ora lamayesero cikhulupiriro cace cida ima nji ndipo Mulungu samgwiritsa mwala. Sicinali cifuniro ca Mulungu kuti Isake aperekedwe nsembe. Mulungu akana nsembe za anthu. (Ezekieli 16:1-2,21). Mu cinthuci Mulungu sanali kungomuyesa Abrahamu ai komanso kumuphunzitsa zomwe zidzaoneke akadzabwera Yesu. Mulungu anali kudzapereka Mwana wace nsembe cifukwa ca macimo athu. Paulo anena za Mulungu kuti, "Iye amene sanatimana Mwana wace wa Iye yekha, koma anampereka cifukwa ca ife tonse." (Aroma 8:32).

## 3. MASO A ABRAHAMU ANALI KUPENYA M'MWAMBA

Abrahamu anali wolola kusiya kwawo, banja lace ngakhalenzo kupereka mwana wace wa iye mwini cifukwa maso ace sanali kupenya za dziko lapansi Ciyembekezo cace ndi cuma cace zinali m'mwamba. Yesu anati, "Kumene kuli cuma canu, komwekonso kudzakhala mtima wamu."(Mateyu 6:21).

Pali nyimbo ya Cikristu yomwe ikuti:

"Kwathu sipadziko, Ndingopitilira."

Buku Lopatulika likuti Abrahamu, "Ndi cikhulupiriro anakhala mlendo ku dziko la lonjezano, losati lace, nakhalira m'mahema pamodzi ndi Isake ndi Yakobo, olowa mnyumba pamodzi ndi iye a lonjezano lomwelo; pakuti analindirira mudzi wakhala nao maziko, mmisiri wace ndi womanga wace ndiye Mulungu." (Ahebri 11: 9-10).

MAFUNSO:

1. Kodi ndi ziani za cikhulupiriro zomwe Mulungu afuna kuti ine ndimucitire?

2. Kodi ndi mu zinthu ziti zomwe ndinali kumukaika Mulungu?

3. Kodi ziyembekezero zanga zaima kuti, pa dziko lapansi pano kapena ku mwamba?



adatenga malo a mtumika (kapolo). Kuitana kocokera kwa Mulungu ndi kuitana kwa ku utumiki osati kuti tionjezere kumveka kwathu eni ai. Ndi cinthu cacisoni kwambiri kuti alipo anthu monga Diotrefe m'mipingo yathu yambiri, amuna omwe amakonda kudzika iwo eni kukhala oyamba ndipo anthuwa amacita zinthu zambiri zoononga nchito ya Mulungu.

3. MMENE ANGAKHALIRE WOPHUNZIRA

Ngati Yakobo ndi Yohane anaphunzira phunziro limodzi mwa pang'ono pang'ono anaphunziranso phunziro lina mwa msanga. Nthawi zina ngakhale zocita molakwika zathu zingakhale ndi zinthu zina zomwe Yesu angadzisandulize kukhala zabwino. Mkhalidwe wao wa mitima ya sontho udawapangitsa kuti atsatire Yesu mwacangu. Mu Luka 5:1-11 tiwerenga momwe mlembi adafotokozera momwe iwo adaitaniridwa. Koma mudaona kusiyana komwe mlembi aliyense wa Uthenga adaonera kusiyana kwa anthu ndi zinthu zomwe zidacitika, kotero kuti zonsezi zitipatsa cithunzi kusiyana ndi momwe zikadakhalira ngati zikadalembedwa mu Uthenga umodzi wokha.

Luka atiuza kuti Yakobo ndi Yohane anali limodzi ndi Simoni ndi Yohane mu nchito yao ya usodzi wa nsomba. (Luka 5:10). Ndi cinthu codabwitsa kwambiri kuti amuna anai onse analandira kuitana kwa Yesu. Cinthu cakuti iwowa anali anadziwana kale ndipo kuti anali kugwirira nchito limodzi cidawathandiza kwambiri kugwira nchito pamodzi ngati gulu la ophunzira pa nthawi ya mtsogolo. Utumiki wa Cikristu ndi nchito yogwiridwa ndi gulu. Ngati mungatenge abwenzi anu kuti mucitire limodzi nchito ya Mulungu mudzazizwa kwambiri ndi kusiya komwe kudzacitike.

Mu vesi 10 ndi 11 tiwerenga za kuitanidwa kwawo ndi kuyankha kwawo. Luka atiuza kuti 'iwo anasiya zonse namtsata Iye.' Iwowa pa tsikuli adagwira nsomba zambiri koposa masiku ena, zomwe kucuruka kwace anali ngati maloto.

iwowa anali a mtima wa sontho. Iye anawaca iwo kuti anali'ana a Bingu'. (marko 3:17). Tipeza citsanzo ca kusapirira kwace kwa Yohane mu Marko 9;38 ndi za mkwiyo wace mu Marko 9: 51-55.

Dyera kwa ndi kunyada kwawo tsiku lina kudawapangitsa kulandira cidzudzulo coopsa kucokera kwa Yesu ndi ophunzira ena aja. Mai wawo amene anali wolakalaka kwambiri anayesetsa kuti ana ace apeze malo okoma (abwino) mu ufumu wa Mulungu. (Mateyu 20:20-21). Anawa, omwe anadzala ndi kudzithemba kwa iwo eni, anaganiza kuti ndithudi iwo anali oyenera (vesi 22). Si cinthu cidabwitsa kuti ophunzira ena aja anakalipa.

2. PHUNZIRO LOLIMBA LIPHUNZIRIDWA

Yesu anatenga zimene zidacitikazi kuwaphunzitsa onsewa phunziro. (Mateyu 20:24-28).

Mu kalata wampfupi wacitatu wa Yohane tiwerenga za iye ali kulankhula ndi munthu wina mu mpingo wina, wocedwa Diotrefe "Wofuna kukhala wamkuru wa iwo." (vesi 9). Pa nthawi iyi Yohane adaphunzira phunziro lomwe Yesu adamphunzitsa. Muyeso wa munthu ndithu yemwe adaitanidwa ndi Mulungu ndiwo wakuti ali wodzicepetsa. Munthu wa dziko lapansi nthawi zonze amafunafuna citukuko cakuti iye amafuna kukhala nawo ulamuliro pa anzaçe. M'moyo wa Cikristu timapita pa tsogolò pokhala atumuki a ena.

Yesu ndiye citsanzo cathu copambana ca izizo. Powakakamiza anthu aku Afilipi kuti akhale onthu odzicepetsa ndi a ulemu, anatero Paulo nati, "Mukhale nawo mtima m'kati mwanu umene unalinso mwa Kristu Yesu, ndipo popezedwa m'maonekedwe ngati munthu, anadzicepetsa yekha nakhala momvera kufikira imfa, ndiyo imfa ya pamtanda." (Afilipi 2:5,8). Pa nthawi ya kudya ca kudya ca Ambuye Yesu anaphunzitsanso phunziro limodzimodzi lomweli powerama ndi kutsuka a ophunzira ace. (Yohane 13:5). Iye



MUTU 3

## KUITANIDWA KWA MOSE NDI MULUNGU

LEMBA: Eksodo 3 - 4:20.

VESI LOLOWEZA: *"Koma munthuyo Mose ndiye woposa anthu onse apa dziko lapansi."* *Numeri 12:3.*

*"Odala ali akufatsa; cifukwa adzalandira dziko lapansi."* *Mateyu 5:5.*

Mose anali mtsogoleri wamkuru ndi wopambana yemwe mtundu wa anthu unakhala naye. Iye anali munthu yemwe anali wolimba mtima kutha kuima pamaso pa mfumu ya cikunja ndikunena kuti ayenera kumasula anthu omwe anali kuwasunga ukapolo kuti akhale afulu. Komatu Buku Lopatulika linena kuti Mose anali munthu wofatsa woposa munthu wina aliyense pa dziko lapansi. Anthu ena amaganiza kuti kufatsa ndi kufooka. Komatu Mose sanali wofooka. Kukhala wofatsa ndiko kukhala wodzicepetsa pamaso pa Mulungu. Yesu ananena kuti anthu oterewa 'adzalandira dziko lapansi'. Mulungu amapatsa mphoto ndipo amagwiritsa ncito anthu odzicepetsa.

1. DZANJA LA MULUNGU LINALI PA MOSE KUYAMBIRA PAKUBADWA KWACE

Kukondweretsedwa ndi Mulungu sikuyamba pamene ife tiyamba kuganizira za iye. Dzanlace liri pa ife kuyambira kale ndithu pamene sitinayambe kuganizira za iye. Dzanja losaonekali limatitsogolera ife kuyambira pa kubadwa kufikira pa tsiku lomwe timadza kwa iye ndi kumdziwa iye.

Mose anacinjirizidwa kuti asafe pamene anali mwana mwa njira yo-zizwitsa kwambiri. Nthano ya momwe anabisiridwa mbango kuti asaphedwe ndi yodziwika kwambiri. Mukhoza kuiwerenga mu Eksodo 2. Mulungu anali ndi colinga koma Mose sanadziwe ici ai.

## 2. MULUNGU ANAMPHUNZITSA IYE MU UNYAMATA WACE

Mose analandira maphunziro odabwitsa kwambiri a utsogoleri. Iye anakula monga mwana wa mfumu m'nyumba ya ufumu ya mfumu Farao. (Eksodo 2:10). Iye anali nao maphunziro onse omwe akadakhoza kulandira. Tiwerenga mu Macitidwe 7:22.

> *"Ndipo Mose anaphunzira nzeru zonse za Aigupto; nali wamphamvu m'mau ace ndi m'ncito zace."*

Komabe coposa zonsezi cinali maphunziro ace a uzimu. Kaya munthu ngwa mkuru bwanji, ngati samudziwa Mulungu sali kanthu konse. Mose anafunika kudzicepetsa pamaso pa Mulungu. Kukula kwace komwe anakulira m'nyumba ya mfumu kukadamcititsa kukhala wonyada kwambiri. Ife tidziwatu kuti anali ndi mtima wasontho. Werengani momwe mtimawu udamcititsa kuti acite mu Eksodo 2:11-12.

Atapha munthu Mose anathawa. Iye anathawa napita kumalo akutari, ku dziko locedwa Midiyani. (Eksodo 2:15). Buku Lopatulika li-nena kuti, komatu, munali kanthu kena koposa mantha mu zomwe Mose adacita. Ahebri 11:24-27:

> *"Ndi cikhulupiriro Mose, atakula msinkhu, anakana kucedwa mwana wace wamwana wa-mkazi wa Farao; nasankhula kucitidwa zoipa pamodzi ndi anthu a Mulungu, ko-sati kukhala nazo zokondweretsa za zoipa nthawi; nawerenga thonzo la Kristu cuma coposa zolemera za Aigupto; pakuti ana-penyerera cobwezera ca mphotho. Ndi ci-khulupiriro anasiya Aigupto, wosaopa mkwiyo wa mfumu; pakuti anapirira moli-mbika, monga ngati kuona wosaonekayo."*

Iye anaphunzira kale kuti kukhala mwana wa Mulungu kunali kofunika koposa kukhala mwana wa mwana wamkazi wa mfumu.





# KUITANIDWA NDI MULUNGU KWA YOKOBO NDI YOHANE

LEMBA: Mateyu 4:21-22.
Mateyu 20:20-28.
Marko 3:13-17.

VESI LOLOWEZA: *"Koma amene ali yense aka-funa kukhala wamkuru mwa inu, adzakhala mtumiki wanu, ndipo amene ali yense akafuna kukhala woyamba mwa inu, adza-khala kapolo wanu."*
*Mateyu 20:26-27.*

Dyera ndi kunyada kawirikawiri kumaima m'njira mwa cifuniro ca Mulungu m'miyoyo yathu. Mwa Yakobo ndi Yohane tiona abale awiri mwa iwo momwe macimo amenewa adakhonjetsedwa.

## 1. CIYAMBI COIPA

Yesu aoneka kuti anali ndi kuona kwina koonera anthu kuposa momwe anthuwo aliti pamene adakomana nawo nthawi yoyamba ndi kuti adzakhala anthu otani mtsogolomo. Iye anako-mana ndi amuna, monga Mateyu, yemwe adakhala moyo wa ucimo wooneka ndipo kuitanidwa kwace kosayembekezera kudacititsa kusintha kosaye-mbekezera ndi kusintha kotheratu m'miyoyo yao. Macimo ocitidwa poonekera, monga kunyenga ndi kuba, analetsedwa mofewa koposa 'macimo a m'tseri' a mu mtima, monga dama ndi kusirira.

Yakobo ndi Yohane penatu adacokera mu banja la ulemu komatu silinali banja la bwino konse ai. Tate wao anali kucita nchito yoona mtima ya usodzi ndipo iyeyu adaphunzitsa ana ace kumacita nchito yoyenera. (Mateyu 4:21). Mai wawo mbali ina, aoneka kuti pena anali mmodzi wa akazi opanda mwai omwe amaononga ana awo a amuna. Ngakhale Yesu yemwe adawapatsa dzina losati laolao lomwe lidatanthauza kuti

Mmodzimmodzi pena awiriawiri. Petro anali mlaliki yemwe anali kulalikira kwa anthu ambiri, Andreya anali yemwe anagwira nchito polankhula ndi mmodzimmodzi. Onsewa ali ofunika. Mudziwatu pakadakhala popamda Petro pakadapanda Andreya wokhulupirika.

MAFUNSO:

1. Ndingacite mu njira yotani kuti ndicite bwino nchito yomwe Mulungu wandipatsa lero?

2. Kodi ndiri naye wina mbanja langa yemwe sali Mkristu ndipo ine sindinamuuzapo konse za Kristu?

3. Kodi alipo wina, penatu yemwe ali yekhayekha, yemwe ndingapalane naye ubwenzi ndipo kuti kupyolera mu ubwenziwu ndingawatsogolere kwa Kristu?



Mu dziko la Midiyani iye anakhala mbusa wodzicepetsa. Munali mu ncito yodzicepetsa imeneyi momwe adakomanira ndi Mulungu. Mulungu adaonekera kwa iye mu tsamba loyaka moto. (Eksodo 3:1-6).

Ndi kwa anthu wamba ndi ku malo wamba komwe Mulungu amadzionetsera yekha kwa anthu. Ife tikhoza kumva kuitana kwace pamene ali kutiitana mu mseu kapena m'chire monga momwe angacitire mu nyumba yopempherera.

## 3. KUITANA KWA MULUNGU KUDZACITA UTUMIKI WAPADERA

Anthu a Mulungu a Isarayeli anali kuzunzika kwambiri mu dziko la Aigupto mu ukapolo. Mulungu anafuna munthu yemwe angawapulumutse kucoka m'manja mwa ambuye ao a nkharwe. Ukapolo nthawi zonse ngoipa.

Mu caka ca 1759 munthu wina anabadwa mu dziko la England dzina lace William Wilberforce. Pamene anali mnyamata iye anakhala Mkristu. Iye anathandizidwa m'moyo wace wa Cikristu ndi munthu wocedwa John Newton. Newton anali Mkuru wa ngalawa za m'madzi pamene anali mnyamata. Ngalawazi zinali ngalawa zomwe zinali kutenga akapolo. Iye anali kukakamiza anthu akuda kulowa mu ngalawa yace ndi kuwatenga iwo kunka nao ku dziko la America komwe anakagulitsa ukapolo. Ndipono John Newton anafika pakumudziwa Yesu Kristu Ambuye. Moyo wace unasinthika modabwitsa. Iye anamva kuitana kwa Mulungu kuti akakhale mlaliki wa Uthenga Wabwino.

William Wiberforce anali munthu wodziwa kulankhula kwambiri ndiponso anali mu Nyumba ya Malamulo (National Assembly mu Britain). John Newton anakakamiza William Wilberforce kuti agwiritse ncito mphatso zace ndi malo omwe analipo kuyesa kuthetsa ukapolo. Ndipo William Wilberforce anayamba cincito cakunena zotsutsana ndi ukapolo. Mu caka ca 1807 kugulitsa kwa akapolo kudatha mu maiko momwe munali

ulamuliro wa Angelezi ndipo mu caka ca 1833 mwambo wa kuti munthu adzikhala ndi akapolo udaletsedwa. Analitu anthu a Mulungu omwe anacititsa anthu akuda omwe anali akapolo kukhala afulu, monga momwe kunaliri kuti munthu wa Mulungu ndiye anaturutsa ana a Israyeli kucoka mu ukapolo.

Pamene Mulungu anaitana Mose poyamba, Mose, anawiringula. Iye anali wodzicepetsa kwambiri kotero kuti anaganiza kuti sanathe kuicita ncito yotereyi. Iye anapanga zowiringula zinai.

a. Iye anati sanali wodziwika kokwanira.

*"Koma Mose anati Mulungu, Ndine yani kuti ndipite kwa Farao, ndikuti nditurutse ana a Israyeli m'Aigypto?" (Eksodo 3:11).*

Mose anaonetsa kudzicepetsa kwa ndithu koona, komatu tisamapanga kudzicepetsa kukhala pokanira. Mulungu akhoza kugwiritsa ncito 'opanda pace' a mu dzikoli koposa awo omwe aganiza kuti 'ndi a uje' odziwika. Ndi iye yemwe analankhula kwa Paulo, "Pakuti mphamvu yanga ithedwa m'ufooko." (2 Akorinto 12:9). Anthu onyada alibe ncito kwa Mulungu.

Mulungu anati kwa Mose, "Koma Ine ndidzakhala ndi iwe," (Eksodo 3:12). Icitu ndico cinthu comwe ciri ndi ncito.

b. Mose adati sanalidziwe dzina la Mulungu. Kodi ana a Israyeli angakadziwe bwanji kuti iye anadzadi ndi cilamulo ca Mulungu Werengani Eksodo 3:13.

Dzina lomwe Mulungu adalipatsa Mose linali dzina la cilendo. "Ine Ndine," iye anatero. (Eksodo 3:14). Lidafotokoza ukuru wace wa Mulungu. Iye ndi wamphamvu zonse yemwe ali wamuyaya. Anthu adzamumvera Mose cifukwa ulamuliro wa Mulungu wosatha anali naye. (Eksodo 3:15).



pa nthawi imodzimodzi. (Mateyu 4:18-20). Andreya poyamba iye anali wadziwapo zinthu zina kale za umboni wa Cikristu pamene anali asadaitanidwe kudzakhala wocitira umboni wa nthawi yonse. Kaya Mulungu afuna ife kupitiriza mu nchito zathu za masiku onse kapena kupereka nthawi yathu yonse kucita nchito yapadera ya Cikristu afuna tonsefe kukhala mboni. Ndi kupyolera mu kukhalupirika kwathu mu zomwe tiri kucita pomwe Mulungu amatipatsa ukapitawo waukuru. Mu fanizi la matelente (Mateyu 25:14-30) Yesu aphunzitsa zimenezi. Werengani vesi 21 la ndime imeneyi. Sitimakhala anthu osiyana mwa dzidzidzi ngati Mulungu atiitana ife kuti tikacite utumiki wina wa padera. Ngati takhala tiri osakhulupirika ndi Akristu a ulesi kale, tidzakhalabe osakhulupirika ndi a ulesi mtsogolonso. M'mishonare aliyense amapeza izi kuti noona ndithu. Palibe munthu yemwe amakhala wosinthika pakuloka nyanja kucokera ku America kudza ku Africa kapena kucoka ku Englalande kudza ku Africa. Kukonzetsera kwa bwino kwa kuitana kwa Mulungu sikudikirira kufikira atakuitanani ai koma kukhala wokhulupirika mu zomwe wandipatsa kuti ndicite tsopano lino.

Andreya anali wokhulupirika asadaitanidwe. Sicinthu codabwitsa, cotero, kuti tipeza kuti anali mboni wa bwino mtsogolo mwace. Analitu Andreya yemwe anampeza mwana (mnyamata) uja yemwe anali ndi mikate isanu ndi nsomba ziwiri, zomwe zidacititsa coziziwitsa cija cakudyetsa anthu zikwi zisanu. (Yohane 12:20-22). Filipo aoneka kuti anali wopanda cangu pakuti adziwe cinthu cakuti acite koma pomwe adangomuuza Andreya iwo anatsogozedwa kunka kwa Yesu. Andreya mosakaika anali wodziwa bwino kakambidwe ndi anthu. Sitiyeneratu kuti tikhale alaliki abwino kuti ticite izi. Nzoonatu kuti nthawi zina alaliki abwino amakhala omwe sangathe konse kucita nawo anthu pa zinthu zawo. Ngati ifeyo tiri odziwa bwino kucita ubwenzi ndi anthu tikhozatu kugwiritsidwa nchito ndi Mulungu kwambiri kudzetsa anthu kwa Kristu. Petro anadza nawo zikwizikwi, Andreya

anabatizidwa cifukwa ca cikhululukiro ca macino ace. (Onani Yohane 1:14-28). Yohane Mbatizi anali mphunzitsi wabwino cifukwa iye nthawi zonse anali kuloza kwa Yesu Monga Mpulumutsi wa anthu osati iye ai. (Yohane 1;29-30). Iye adanena kuti Yesu anali Mwana wa Mulungu. (vesi 32-34). Andreya yemwe mtima wace udakonzedwa kale ndi Yohane, tsopano anakhala wotsatira wa Yesu. (Yohane 1;35-37). Cinali cobvuta kwambiri kuti Yohane Mbatizi ataye otsatira ace. Kwa masiku owerengeka iyeyu adzaphedwa ndi mfumu Herode. Komatu sanaphedwa iye asadatsiriza ncito yace. Iye anitanidwa ndi Mulungu kuti adzakonze njira ya Yesu. Kodi ifeyo timatenga kuitana kwa Mulungu kukhala coti tipeze malo apamwamba ndi anthu odziwika kwa ife eni kapena monga njira yomwe tingaonetsere Kristu Kwa anthu? Yohane Mbatizi wokhulupirika anatsogolera Andreya kwa Kristu.

3. ANDREYA WOKOLA MIYOYO

Taonani zomwe zidacitika pomwe Andreya adangopeza Kristu. Anatengera mbale wace kwa Kristu! (Yohane 1:40-41). Iye 'poyamba anapeza.....' Asadacite kanthu kena kali konse anayamba wapita kukauza mbale wace. Yesu nkutitu asadamuitane iye kukhala msodzi wa anthu koma cifukwa ca cinthu codabwitsa comwe cidaoneka kwa iye ayenera kukauza ena. Ife sitifunika kuti tiitanidwe kwa padera kuti tikhale 'okola miyoyo'. Mkristu ali yense aitanidwa kucita nchito imeneyi.

Simoni adakhala wophunzira wa mkuru koposa ena, komatu Andreya ndiye adamtsogolera iye kwa Kristu. Inuyo penatu simungakhale alaliki opambana, pena simungakhale pa malo ofunika (malo akuru) mu mpingo mwanu, koma umboni wanu wokhulupirika ungadzetse atsogoleri akuru a mtsogolo kwa Kristu.

4. ANDREYA WOPHUNZIRA

Andreya anakhulupirira mwa Kristu poyamba koma iye ndi mbale wace anaitanidwa ku nchito



c. Mose anapanganso cokanira cina ponena kuti anthu sadzamumvera kapena kumukhulupirira. (Eksodo 4:1).

Mulungu anamuuza kuti iye adzacita zozizwitsa kupyolera mwa iye Moseyo kolero kuti anthu adzaona kuti Mulungu anali naye.(4:2-9). Ngati tiri atumiki oona a Mulungu anthu adzaona m'miyoyo yathu zisonyezo za mphamvu ya Mzimu Woyera. Iwo adzakhulupirira zomwe tidzalankhula cifukwa ca njira yomwe tikhalira ifeyo.

d. Cokanira cace comariza cakuti sanali wokhoza kulamkhula ndi kulalikira bwino. (Eksodo 4:10).

Yankho la Mulungu linali lakuti ngati waitana munthu amam'patsanso mphatso zakucita ncitoyo. (Eksodo 4:11-12).

Posowa cocita Mose anayesa kuti aleke kuicita ncitoyi. Sanawiringulanso koma anango ngoti, "Tumani munthu wina" (4:13). Ambiri a ife timanenanso cotero. Ife timafuna kuona ncito ya Mulungu iri kukula. Tifuna kuona anthu ali kupulumutsidwa. Koma ifeyo tifuna kuti munthu wina akacite ncito yotereyo. Tiri ngati munthu yemwe anasintha mau a Yesaya (Yesaya 6:8) kuti "Ndine! TUMENI."

Mulungu anakwiya kwambiri ndi kukana kwa Mose kuti akacite cifuniro cace. Ngakhale anamulonjeza thandizo lina. Aaroni mbale wace wa Mose, adzamulankhulira iye. Monga momwe womasulira amamasulira m'mishonare yemwe sadziwa cilankhulidwe ca anthu, cotero Aroni adzakhala woturukila mau osamveka kwambiri a Mose. (Eksodo 4:10-16).

Mose nthawi iyi adamvera. (4:18-20).

Cifukwa Mose anali wofstsa kwambiri iye anaganiza kuti sakadamvera kuitana kwa Mulungu. Mulungu adamuinetsa kuti, pamene iye aitana, amapatsanso zida zonse zofunikira. Monga

momwe Paulo anati, "Ndikhoza zonse MWA IYE WONDIPATSA MPHAMVUYO." (Afilipi 4:13).

MAFUNSO:

1. Kodi ndiri wodzicepetsa kokwanira kuti Mulungu akhoza kundigwiritsa ncito?

2. Kodi ndiwiringura bwanji poyesa kucita cifuniro ca Mulungu?



MUTU 10

## KUITANIDWA KWA ANDREYA NDI MULUNGU

LEMBA: Mateyu 4:17-20.
Yohane 1:35-41.

VESI LOLOWEZA: *"Anayamba iye kupeza mbale wace yekha Simoni, nanena naye, 'Tapeza ife Mesiya...'" Yohane 1:41.*

Ngatitu panali kusiya kwa abale awiri kunali pakati pa Simoni ndi Andreya. Koma ngakhale zinali tero Yesu adawaitana onse awiriwa kukhala asodzi a anthu.

1. KUMPAMBANA ANDREYA

Simoni anali munthu wa mphamvu kwambiri kotero kuti anampambana (anamcita mthunzi) Andreya. Simoni anali mtsogoleri wa cibadidwe; Andreya anagotsatira. Penatu pamene iwowa anali ana Simoni ndiye amene anali kusankha masewera omwe angasewere, Simoni yemwe anali kuyankha mafunso ku skulu, Simoni yemwe....... nthawi zonse Simoni! Nthawi zina ncobvuta kwambiri kukhala ndi mbale wonga Simoni. Nthawi zambiri Andreya sanali kuitanidwa ndi dzina locelace. Anali 'mbale wa Simoni'. (Yohane 1:40). Ndipo pamene anakhala ophunzira a Yesu Petro anali mmodzi wa atsogoleri omwe nthawi zonse anali kupezeka ali ndi Yesu; Andreya anali mmodzi wa ophunzira wonga ena aja onse.' (Onani Mateyu 17:1 ndi Mateyu 26:36-37).

2. ANDREYA MTSOGOLERI

Panali nthawi imodzi yofunika kwambiri pomwe Andreya anatsogola. Iye ndiye anali woyamba kumtsatira Yesu. (Yohane 1:35-37,40).

Andreya aoneka kuti anali wokondweretsedwa ndi cipembedzo koposa Simoni. Yohane 1:35 atiuza iye anali ali wophunzira wa Yohane Mbatizi kale. Ici citanthauzwa kuti iye

Zidamcititsa kukhala wodzicepetsa ndipo pamene adakomana ndi Yesu atauka kwa akufa anali Petro wosiyana. Iye adakana kuitanidwa kwace koma Yesu adamtumiza iye. (Werengani Yohane 21:15-17). Simoni munthu wamkhalidwe wosapembedza anakhalano Petro, Mtumwi, mmodzi wa atsogoleri akuru koposa mu mpingo woyamba. Pa tsiku la Pentekositi Mulungu adagwiritsa nchito kulalikira kwace kudzetsa anthu zikwi zitatu (3,000) kwa Kristu. Mulungu ali wokhoza kuitana ndi kugwiritsa nchito anthu omwe sayembezeredwa konse ai mu utumiki wace. Nanga bwanji inuyo?

MAFUNSO:

1. Kodi umudziwa wina monga Simoni yemwe ndingamamupempherere?
2. Kodi Mulungu Amasintha bwanji miyoyo ya anthu?



MUTU 4

## KUITANIDWA KWA ARONI NDI MULUNGU

LEMBA: Eksodo 4:10-16,27-31.
Eksodo 32: 1-6.

VESI LOLOWEZA: *"Ndipo Aroni anawafotokozera mau onse amene Yehova adauza Mose, nacita zizindikiro zija pamaso pa anthu."* Eksodo 4:30.

Nthawi zina Mulungu amaitana munthu wina Kuti akathandize munthu wina inde ngakhale munthu wamkuru kwambiri yemwe. Akuru ambiri ankhondo amadalira kwa ao amene ali aciwiri kwa iwo.

Ndi cinthu colimba kutenga malo akukkala waciwiri, komatu ici ndico comwe Aroni adaitaniridwa kuti adzacite. Aroni sanali wamkuru koposa monga momwe analiri mbale wace koma anali wofunika kwambiri ku ncito ya Mulungu. Mulungu samapatsa mphatso zace zonse kwa munthu mmodzi ai Ngati akadatero munthu akadakhala wonyada kwambiri ndipono nakhala wopanda ncito pamaso pa Mulungu. Ngakhale Mose yemwe anasowa mphatso imodzi ndipo mphatso imeneyi Mulungu adampatsa Aroni.

### 1. ARONI ANALI MPHATSO YA MULUNGU KWA MOSE

Aroni anali mbale wace wa Mose, koma zaka zambiri analeka osakhala malo amodzi. Mose anali kukhala ku Midiyani, kuweta nkhosa, pamene Aroni anali kugwira ncito yolimba ya ukapolo mu Aigupto.

Tidaphunzira mu Mutu wapita momwe Mulungu adaitanira Mose kuti akatsogolere ana a Israyeli kuturuka mu dziko la Aigputo. Iye anali munthu wa nzeru. Anakhala mtsogoleri wa mkuru. Koma sanali wokhoza kulankhula pa misonkhano ikuru ikuru ya anthu. Sanali kutha kulankhula bwino. Kodi nanga adzatha bwanji kumukakamiza Farao kuti akalole ana a Israyeli

kuturuka, ngati sakadatha kukalankhula mu njira yomwe angakanene naye Farao kuti amve bwino? Akadacita bwanji kuti ana a Israyeli am'tsatire ngati sakadatha kuzindikiritsa kuti ici cinali cifuniro ca Mulungu?

Nzeru za Mulungu nzodabwitsa kwambiri kuti ngakhale pamene Mose anali kumafunsowa Aroni anali pa ulendo wace wakudza kudzakomana naye. (Eksodo 4:10-14).

Sitidziwa cifukwa ciani Aroni anali kudza kudzamufuna Mose. Kapena iye anaona kuti mbale wace ndiye anali wokhoza kuturutsa ana a Israyeli kucoka mu ukapolo ndipo anali kudza kuti adzam'kakamize kuti akatero. Ndikaika ngati adadziwa somwe Mose adzamufunsa kuti acite. Koma Mulungu anadziwa kusowaku ndipo Mulungu anaitana Aroni kumuka ku Midiyani mu nthawi yomwe anali kufunika. Oalibe kukaika kuti ndiye adaika mwa Aroni maganizo akuti Aroni apite kwa mbale wace. Aroni adamvera. (Eksodo 4:27). Mulungu salakwatu. Iye amakhala ndi munthu woyenera kucita ncito yoyenera ndi pa nthawi yoyenera. Taganizani momwe Aroni akadaonongera nzeru ya Mulungu akadakana kumvera kuitana kwace.

2. ARONI ADAYENERA KUPHUNZITSIDWA

Mulungu adauza Mose kuti Aroni "adzamulankhulira iye kwa anthu" ndikuti Mose adzakhala 'ngati Mulungu' (Eksodo 4:16). Iye sadatanthauza kuti Aroni adzimulambira Mose ai. Iye adatanthauza kuti Mulungu adzalankhula kupyolera mwa Mose polankhula ndi Aroni, pomwe Mose adzalankhula kwa anthu kupyolera mwa Aroni. Aroni anali mlaliki wamkuru koma sanali munthu woganiza kwambiri ai. Ena a ife tiri ocenjera polankhula ndi anthu ena. Pena Mulungu adatipanga kukhala omwe tingapalane ubwenzi ndi anthu ena msanga kotero kuti anthu angatimvere ife. Koma timamva kuti sitikhoza kulankhula za Kristu cifukwa sitiri anzeru kwambiri kukhoza kuphunzira Buku Lopatulika tokha. Timapeza kuti ndi colimba kwa mbiri



Simoni akalibe wobvutika ndi wosangalatsidwa ndi muja adakomanira ndi Yesu adapita kukamveranso zomwe anali kulankhula kwa nthawi yaciwiri. Sukufunikatu kuti umuke ku calici kuti ucite zinthu zoterezi ai. Yesu adapita komwe kunali anthu ndipo, monga momwe anthuwo adafunira, anakhala pansi pa maudzu kumvetsera. Ngakhaletu panali ci unyinji ca anthu koma cimamveka ngati ali kulankhula kwa iwe wekha. Iye analankhula za cikhululukiro ca macimo, analankhula za molo omwe acedwa ufumu wa Mulungu komwe cilungamo ndicoonadi zinali kulamulira, analankhula za Mulungu kuti amasamalira zonse za moyo wathu. (Werengani mbali imodzi ya ciphunzitso ca pa phiri mu Mateyu 6:25-34). Simoni anadziwa kuti zinali kumulowa ndipo sanatsimike konse ai kuti analidi kufuna kukhala monga momwe analikumveramo. Pakuti iyeyu sanali munthu wa mkhalidwe woti angakhale wacipembedzo.

Ndipo tsiku lina pomwe anali wotanganika ndi nchito yace mungalawa yace osati kutari ndi mbali mwa madzi anamva mau aja kaciwiri. Ali kumuitana, kumkakamiza, anadza kucokera tsidya lamadzi, "Unditsate Ine ndipo ndidzakusandutsa msodzi wa anthu." (Marko 1:17).

Petro anadziwa kuti panalibenso kukaika ndikumaganziza zina. Kaya ndi cipembedzo kapena ai koma adayenera kutsatira ndi kumvera. Tiwerenga kuti "Nthawi yomweyo anasiya mapsasi ao namtsata Iye." (vesi 18). Pomwetu Petro watsimikiza kuti acite kanthu basi amatsimikizidatu kotheratu.

Petro sadakhala woyera tsiku limodzi. Iye analakwa kambirimbiri. Mulungu adacita nchito ya ikuru pa moyo wace, kusema tidzidutswa tating'ono kucoka pa thanthwe. Nthawi zambiri anatsegula pakamwa pace mwa cangu ndipo analankhula zinthu zolakwika. (Werengani Luka 9:28-35, Marko 8:31-33 ndi Marko 14:66-72). Petro analephera koopa pokana Mbuye wace. Komatu Mulungu adacititsa kulephera kwaceku kumpanga kukhala munthu wa bwino koposa.

wosiyana ndi iye anali wa cidwi ndi malalaliki wamphamvuyu, ndipo anali kumayemda naye nthawi zambiri. Ndipo comweco anakomana ndi Yesu poyamba ndipo tsiku lina anadza mwaliwiro kudza kwa Simoni ali wa cisangalalo ndi wokodwera kwambiri. "Tampeza iye," iye anapfuula, "Tampeza iye....." "Mwampeza yani," anafunsa Simoni. "Tampeza Mesiya." (Onani Yohane 1:42). Mesiya ndilo linali dzina lomwe lidapatsidwa kwa Mombolo yemwe Ayuda anali kumuyembekezera. Malemba ao analonjeza kuti tsiku lina adzaza ndipo adzakhala mfumu yao ndi kuwaombola iwo kucoka kwa adani ao. Koma panali anthu ena azipembedzo omwe abadza nadzanamiza anthu kuti iwo anali Mesiya ndipo Petro anali be nao nchito anthu oterewa. Komatu Andireya anali wokondwa ndi wanthumazi ndi cinthu cine ndipo cotero Simoni adamuka naye pamodzi. (Onani Yohane 1:42). Iye anamuka atadzazidwa ndi kusakhulupirira ndi wokonzekera kukanyodola koma pomwe adangokomana ndi Yesu anadziwa kuti munali kanthu kena kosiyana mwa iye. Munali mphamvu ya mkhalidwe, ulamuliro, womwe unali wosaonekaoneka. Koma pamene analankhula Petro anabvomezera monga anthu ena onse ambiri kunena kuti, "palibe munthu analankhula cotere monga uyu." (Onani Yohane 7:46). Ndipo pomwepo, maso aja, anaoneka ngati anali kusanthula mkati mwa Simoni kuona zinthu zonse za iye ndipo pomwepo anati, "Ndiwe Simoni mwana wa Yohane? Udzacedwa Kefa (ndilo losanthulika Petro)." (Yohane 1:42). Kodi anatanthauzanji? Petro.....tanthwe? (Ndilotu tanthauzo lace la dzinali). Iye analidi wolimba unde; koma osati wolimba woti wina aliyense wa cipembedzo an fanene kuti wolimba monga thanthwe. Ngati Yesu anali kufunafuna womtsatira iye kukhulupirira mwa Simoni anali kulakwa kwakukuru.

Petro ananyamuka namuka kwao atakhudzidwa ndi mphamvu ya munthuyu komanso anali wosokonezeka.

3. KUITANIDWA KUKHALA WOPHUNZIRA

Milungu ina idapitapo ndipo pa nthawi imeneyi Yesu adayamba nchito yace ya kulalikira.



kumvesetsa. Ici ndico cifukwa Mulungu adaperekera abusa ndi aphunzitsi ku mipingo yace. Iye amawapatsa iwo luntha lakukhoza kuphunsira Mau ace kotero kuti iwo akhoza kutiphunzitsa ife ndipo ifeyo tidzapitiriza mauo kwa anthu ena.

Aroni anafunika kukhala wofatsa kwambiri kuti aphunzitsidwe ndi Mose. Kodi ife tidziwa kuti Mulungu angapatse nzeru kwa anthu ena kotero kuti ife tiphunzire? Kodi timayamika Mulungu cifukwa ca abusa athu ndi aphunzitsi kapena timangowanenanena pa zocita zawo?

3. ARONI ANALI KUFUNIKA KUKHALA CIFUPIFUPI NDI MOSE

Nthawi zonse pamene Mose anali pambali pace pa Aroni anapambana. Aisrayeli anakhulupirira Mose cifukwa cakulankhula kwa mphamyu komwe Aroni adalankhula naoo. (Eksodo 4:29-31). Aroni adalankhula ndi ulamuliro wonse kwa Farao kotero kuti mfumu ya nkharweyi idamvetsera. Mukdoza kuona mphamvu zace za mau ace motere, "Atero Yehova, Mulungu wa Israyeli; Lola anthu anga apite, kundicitira madyerero m'cipululu." (Eksodo 5:1). Sunali ulamuliro wa Aroni ai, Ulamulirowo udacokera kwa Mulungu kupyolera mwa Mose. Ulamuliro wathu ndiwo Liu la Mulungu.

Mulungu adagwiritsa Aroni ncito mu njira zina kuthandiza mbale wace. Pameme Amaleki anadza kudzamenyana nkhondo ndi a Israyeli Mose adaima pamwamba pa phiri ndi ndondo m'manja mwace yomwe Mulungu adampatsa Pamene adanyamula ndondo ija a Israyeli anali kupambana. Koma mikono yace idalema ndipo anagwetsa manja ace. Pomwepo a Amaleki anayamba kupambana. (Eksodo 17:18-11). Ndipo comweco Aroni ndi Huri, anamgwirizitsa Mose manja ace comweco Israyeli adalakika. (Eksodo 17:12-13).

Mose adasowa Aroni ndipo pamene Aroni anali ndi Mose anali wofunika kwambiri ku ncito ya Mulungu. Pamene Mose wacokapo Aroni anali

kulephera. Pamene Mose anali pa phiri la sinai kulankhula ndi Mulungu Aroni adafooka. Iye adamvera zopempha zonyansa za anthu kuti awapangire milungu ina. Ndipo iye anawapa= ngira ka mwana ka ng'ombe ka golide nawatso-golera pakucipembedza. (Eksodo 32:1-6). Ndipo anadzetsa cilango coopsa kwa anthuwa ndi ukali wa Mulungu pa iye mwini. (Eksodo 32:21-24). Taonani kuwiringura kwace kopanda pace. Iye anadziwa kuti anacimwa.

Titsimikiza kuti Aroni analapa macimo ace ndikuti Mulungu adamukhululukira cifukwa ada-pangidwa kukhala Mkuru Wansembe. (Eksodo 40: 12-15). Uwutu unali mwai waukuru kwambiri ndi wodabwitsa. Mkuru Wansembe adaima pakati pa Mulungu ndi anthu omwe anali kupereka nsembe za macimo ao. Pamene Yesu anadza anasanduka Mkuru Wansembe wathu. Kotero kuti Aroni ndi ana ace analowa malo a Yesu mpaka kufikira Iye mwini anali wokonzeka kudzawatenga malo ace mwini. Codabwitsa kotani cikhululukiro ca Mulungu!

Kupatsa munthu wocimwa monga Aroni mwai woterewu. Mulungu sadaiwale kumvera kwace kwa Aroni ku kuitana kwace ndi kukhulupirika kwace kwa Mose. Mulungu sakhala ndi mangawa ndi anthu. Iye amapatsa modabwitsa mphatso ya utumiki wokhulupirika.

MAFUNSO:

1. Kodi ndi mphatso yanji yomwe Mulungu anandipatsa? Kodi ndiri kuigwiritsa ncito?
2. Kodi ndiri wolola kutenga malo aciwiri kwa atumiki ena a Mulungu?
3. Kodi ndi phunziro lanji lomwe ndingaphu-nzire kucokera mu kulephera kwa Aroni pamene sanali pamodzi ndi Mose?



akadawasirira konsa. Ambiri a iwo anali onye-nga. Iwo anali kuoneka kuti anali kukondwere-tsedwa ndi kuweruza ena kuposa kuwathandiza ndipo mosakaika Petro anali mmodzi wa odzudzu-lidwawo.

Iai - Simoni sanali munthu wamkhalidwe wakuti angaitanidwe ndi Mulungu. Iye ndi atso-goleri a zipembedzo onse akadagwirizana paici. Kodi nanga nciani cidampangitsa kukhala mlaliki?

2. KUKOMANA KWACE NDI YESU

Cikadakhala cinthu cobvuta kukhala mu Galileya monga adacitira simoni kuti asamve za Yesu. Kukhala mu Galileya kunali kanthu kena monga kukhala pafupi ndi Nyanja ya Kariba ka-pena Nyanja ya Banguelu. Linali dera la mata-uni ndi midzi ya ing'onoing'ono. Munalibe zinthu zambiri zinali kucitikamo ndipo mlaliki wa cilendo analidi mbiri yodabwitsa. Anthu omwe anali alimi anakondwera kusiya zida zoli-mira zao pansi ndi asodzi kusiya mapsasa ao pansi kumuka kukamvetsera kwa nthawi ya ora limodzi kapena kupambabapo. Azimai anali atopa pakumalankula akhani imodzimodzi pamene anako-ma pa citsime kapena pomwe akhala kuzungulira miphika yao yophikira. Ici cinali cinthu cina cosiyana ndithu. Ndipo cotero nkhani zidaya-mba ndi mau akuti, "Kodi wamva muja wa.....?", ndikunena zina za zozizwitsa za kuciritsa zomwe Yesu adacita. Yesu anakhala mbiri yoti ngakhale Petro yemwe sadatha kunyozera kuti ndani munthu ameneyu. Pakutha zonsezi Yesu sanali monga a rabi omwe anatha nthawi ya itari ya moyo wao pakuwerenga mabuku. Iye anali munthu wonga anthu ena onse a ncito yemwe ada-peza zakumuthandiza zace pakugwira nchito ndi manja ace pomapala matabwa.

Simoni anali nao mwai woyambirira wakuko-mana naye Yesu, ngakhale pamene anali asadadzi-wike kwambiri. Yohane Mbatizi anali kumveka mbiri za masiku amenewo. Andireya, mbale wace wa Aimoni, yemwe anali munthu wamkhalidwe

MUTU 9

## KUITANIDWA KWA PETRO NDI MULUNGU

LEMBA: Yohane 1:35-42.
Marko 1:16-18.

VESI LOLOWEZA: *"Ndipo Yesu ananena nao, Idzani pambuyo panga, ndipo ndidzakusandutsani inu asodzi a anthu." Marko 1:17.*

Pamene Yesu adaitana ophunzira ace khumi ndi awiri adasankha anthu a makhalidwe osiyanasiyana. Mosakaika iye anafuna kutionetsa kuti kuli malo a munthu wa mtundu uliwonse mu ufumu wace. Simoni, yemwe Yesu adamucha dzina lakuti Petro, anali munthu yemwe sanali wacipembedzo.

1. MKHALIDWE WA MUNTHU

Simoni anali munthu yemwe mukadatha kumuona ngakhale ali pa cigulu ca anthu. Iyeyu anali munthu wamkuru, ndi minofu yace inali yaikurunzo, yomwe inakula cotere ndi nchito yace yokoka mapsasa ogwirira nsomba. Mbali zonse iyeyu analidi munthu weniweni, wodziwika kwambiri ndi asodzi a mbali yomwe anali kukhala ndiponso yemwe anyamata anali kumsirira, komatu anali munthu yemwe simungaganizire kuti mungampeze ali m'nyumba yopempherera. Ngati inu tsiku lina mukadanena kwa iye kuti adzakhala mlaliki ndithu akadaseka kwakuti misozi mbwee. Iyeyu sanali monga anthu ena ofatsa, aulemu aziphunzitsi (alaliki ndi aphunzitsi) a masiku aja. Iyeyu anali munthu wankhwimbi, wonunkha pfungo la nsomba ndipo mwa iye munalibe kanthu kena komwe munganene kuti wodzuka kapena wophunzira. Kutukwana kunaturuka pakamwa pace kawirikawiri koposa kupemphera. Ndikaika ngati adapita ku nyumba yopempherera konse. Pena anali kuganiza kuti cipembedzo cinali ca bwino kwa ana ndi akazi koma osati kwa amuna enieni. Atsogoleri a zipembedzo a masiku amenewo sanali anthu omwe Petro



MUTU 5

## KUITANIDWA KWA YOSWA NDI MULUNGU

LEMBA: Numeri 14:16-12; 26:30,
Numeri 17:18-23.

VESI LOLOWEZA: *"Ndipo Yehova anati kwa Mose, Utenge Yoswa mwana wa Nuni, ndiye munthu mwa iye Muli mzimu, nuike dzanja lako pa iye." Numeri 27:18.*

Mulungu amaitana anthu ena omwe ali kunia kwa mpingo kuti akhale atumiki ace. Kawiriwiri, amatenga anyamata omwe ali kukula m'ciyanjano ndi anthu a Mulungu. Monga mbeu m'munda wosungidwa bwino miyoyo yao imasamalidwa ndi kukonzetseredwa bwino lomwe. Yoswa anali munthu wotereyu. Iye anali nao mwai waukuru wakukhala pansi pa cikoka ca mtsogoleri wa mkuru ndi wa umulungu, Mose.

1. KUKONZEKERA KOYAMBIRIRA

Sitiuzidwa konse za moyo wace wa ubwana wa wa Yoswa koma tidziwa kuti iye anakula pa nthawi yomwe ana a Israyeli anali paulendo wao wopita ku Dziko la Lonjezano. Monga mnyamata anaona cinthu cozizwitsa cija pamene madzi a Nyanja Yofiira anaima monga khoma, nasiya njira yakuti iwo ayendemo. Zaka zonse zamtsogolomo iye anali kumakhala pamodzi ndi akuru akuru ace pozungulira moto ndi kumanena za momwe iwo analiri akapolo ndi momwe Mulungu adawalanditsira. Iye sadatha kuzemba kuti iye anali mmodzi wa anthu a mtundu wa padera womwe unakonzedweratu ndi Mulungu. Zoonetsera dzanja la Mulungu kwa anthu ace zinawazungulira iwo.

mosakaika kuyamikira ndi kusulira mtsogoleri wao Mose zinakhudza kwambiri moyo wace. Kumaona munthuyu wa pemphero ndi wa cikhulupiriro kuti anali tate wa kwa mtundu wonse, kuima nji kutsutsana nazo zonse zobvuta zocokera kwa adani ndi kwa anthu ena mwa Israyeli

momwemo omwe sanali kukwanitsidwa ndi zocita zace, zidamcititsa iye kumtsatira Mulungu ndi mtima wace wonse. Ngati anthu onse akuru akadadziwa za momwe miyoyo yao kuti imacita citsanzo cotani kwa anthu ainyamata.

Nthawi yace yoyambayamba kuonetsa cidwi cace inadza pamene Mose adampatsa Yoswa kulamulira gulu la nkondo ndi kumuuza kuti akamenyane ndi a Amaleki. (Eksodo 17:8-9). Ici cidampatsa phunziro lalikuru lakukhulupirira mwa mphamvu ya Mulungu yokha kuti apambane nkhondo zace. M'mene Mose anali cinyamulire manje ace ndi kupemphera kwa Mulungu ana a Israyeli anali kupambana kwambiri, koma ngati Mose agwetsa manja ace pansi, a maleki amayamba kupambana. (Eksodo 18:11-13).

Umulungu ndi kukhulupirika kwa mnyamata uyu Yoswa sikudabisika konse ai. Tsiku linafika lomwe Mose anatumiza mthenga kukamuitana ndi kumuuza kuti afuna kuti iye akhale mtumiki wacewace. Unali mwai waukuru kwambiri kuti munthu angamakhale cifupifupi ndi munthu wamkuru wotere! Ndi maphunziro otani a uzimu omwe akadaphunzira.

Kukhala kwace cifupifupi ndi Mose kudamcititsa kudziwa zazikuru zambiri m'moyo mwace monse. Mulungu adaitana Mose kuti akwere mu phiri, phiri Sinai, kuti akalankhule naye ndi kumupatsa Malamulo Khumi. Monga mtumiki wace Yoswa adapita naye. (Eksodo 24:12-13). Ulemerero wa Mulungu udaonetseredwa mu njira yakuti pa phiri paja maonekedwe a Mose adasandulika. Nkhope yace idawala momwe anali kuonetsera ulemerero wa Mulungu mwa iye.(Eksodo 35:29-30). Sitiuzidwa zomwe zidaoneka kwa Yoswa koma zinthu zoteresi zidanyamula m'mwamba kwambiri cikhulupiriro cace. Koma Cipangano Catsopano citiuza kuti kuyambira paja adafika Yesu Mkristu aliyense angacite monga momwe zidaoneka kwa Mose, pamene Mzimu Woyera aonetsera ulemerero wa Mulungu m'mitima mwathu. Paulo anena kuti, "Koma ife tonse ndi nkhope yosaphimbika popenyerera monga mwa kalilore



Mulungu adaika dzanja lace pa iye. (vesi 9). Ngati Mulungu atiitana ife ndipo ife timvera adzaika dzanja lace pa ife. Ife tidzadziwa kugwira kwace kwa mphamvu. Zomwe kale zinali kuoneka kuti nzosatheka kucitika zidzakhala zotheka cifukwa tiri kupita m'mphamvu ya Ambuye.

MAFUNSO:

1. Kodi anthu a dziko lapansi ali ndi mkhalidwe wotani?

2. Kodi ndi mkhalidwe wa umunthu wotani womwe Mulungu auwerengera?

3. "Mulungu ali nafe.....adzatitsutsa ndani?" (Onani Aroma 8:31-39).

Ambuye anali ndi nzeru zina. Iye anafuna Davide, wa mng'ono mwa onse, mbusa yemwe onse sadamsamalira za iye kuti angawerengedwe. Mu Samueli Woyamba 16:6-12 tiwerengamo phunziro lopambana kwambiri la momwe Mulungu amaweruzira anthu. Onani pa vesi 7 kwenikweni.

Kodi timacita dama ndi mphatso zathu ndi m'mene tingagwirire nchito? Kodi anthu ena amatiyamikira? Mulungu asadatigwinitse nchito angatisinthe ife mu njira yomwe ingakhale yowawa pena Kapena timva kuti sitikhoza kukhala a mphindu konse kwa Mulungu cifukwa akuti sitiri oyenera? Comwetu Mulungu adacipanga poyamba angacipangenso.

3. MUNTHU YEMWE MULUNGU ADAMKONZERA

Ngakhale anaoneka ngati wosayenera Mulungu anakhala ali kumukonzetsera Yeremiya kwa nthawi ya itari. Iye adamsankha iye kuti adzacite nchitoyi ngakhale pamene anali sanabadwa! (vesi 5). Mulungu amacita cinchito copambana ca kukonzekera nchito yace.

Mulungu adamuika iye m'banja la umulungu momwe iye akadaphunzira za njira zace kuyambira pa ubwana wace. (vesi 1). Yamikani Mulungu cifukwa ca makolo a Cikristu. Kodi banja canu ndi banja lomwe Yeremiya akadaphunzitsidwamo?

Milungu adalankhula kwa iye kupyolera m'Mau ace. (vesi 2 ndi 4). Kodi tiwakonda mau a Mulungu ndi kuwawerenga kawirikawiri?

Mulungu anamlonjeza kuti adzampatsa mau akuti alankhule. (vesi 7).

Ndiponso anamulonjeza kuti adzamsunga iye mkati mwa zobvuta zonse. (vesi 8 ndi 19). Palibe wina aliyense wa ife yemwe angafe kufikira Mulungu watsiriza nchito yace kupyolera mwa ife. Kukhala nalo lonjezano la Mulungu kukadakhala kokwanira kwa kanthu kali konse. Iye sanena bodza.



ulemerero wa Ambuye, tisandulika m'cithunzithunzi comweci kucokera kuulemerero kunka kuulemerero, monga ngati kucokera kwa Ambuye Msimu." (2 Akorinto 3:18).

2. CIKHULUPIRIRO CIYESEDWA

Potsiriza nthawi idafika pomwe ana a Israyeli adafika m'malire a Dziko Lalonjezano. Panafunika anyamata olimba opanda mantha kuti amuke kukazonda dzikolo. Iwotu nkuti akakomana ndi zoopsa kucokera kwa adani, ndipo cotero amuna okha acikhulupiriro ndiwo anali kufunika kumukako. Tsopanotu cinali cinthu cosakaikika kuti Yoswa adzakhala mmodzi wa amuna omwe adzapitawo.

Nyengoyi idaonetsera cinthu ca cikuru kwa iye cifukwa pa nthwi imeneyi dzina lace lidasinthidwa. Kufikira pa nthawi imeneyi dzina lace linali 'Hosheya', lomwe linatanthauza kuti 'thandizo' kapena kuti 'cipulumutso.' Mose adampatsa dzina lakuti Yoswa, lotanthauza kuti 'Ambuye ndiye cipulumutso.' (Numeri 13:16). Monga munthu wina aliyense wa Mulungu Yoswa anayenera kuti aphunzire kuti iye adzatsamira kotani mu thandizo la Mulungu osati mwa iye yekha. Kuyesedwa kunali kudza. Nthawi zonse mwai umadza ndi zincito zoyenera kucitika ndipo kawirikawiri zimakhala zobvuta. Yoswa anayenera kuphunzira kuti zija zidaoneka pa phiri ziyenera kutsatiridwa pakuyesa mu dambo.

Atatha kulizonda dziko lija kwa masiku makumi anai anyamata aja anabwerera kwao. Ambiri a iwo anaonetsera kuti cikhulupiriro cao cinali cocepa kwambiri. Iwo anabvomereza kuti Kenani linalidi dziko lokoma kwambiri koma ananena kuti adaniwo anali amphamvu kwambiri kuti angawagonjetse. (Numeri 13:27-28, 31-33). Taonani cikhulupiriro cacing'ono mwa anthu omwe anali ndi Mulungu wamkurukuru, Mulungu yemwe adawalanditsa kucoka mu dziko la Aigupto!

Yoswa yekha ndi Kalebi ndiwo anali ndi cikhulupiriri cacikuru kucita ncitoyo, (Numeri

13:30; 14:6-9). Monga amuna a cikhulupiriro masiku onse anapeza kuti iwo anali patsogolo kwambiri ndi anthu a Mulungu kotero kuti iwowa analimbana nao mtsutsano. Zinthu zidaipa kotero kuti anthu anali kuopsetsa kuti adzawaponya miyala. (Numeri 14:10). Yoswa anali kuyambayamba kuphunzira kucita nao mazunzo a msilikari wa bwino wa Kristu Yesu.' (2 Timoteo 2:3).

3. MSILIKARI WABWINO ALANDIRA MPHOTHO

Cifukwa cakuukira Mulungu kawirikawiri ndi kusakhulupirira kwao,themberero lidaikidwa pa ana a Israyeli. Iwo sadzalandira Dziko la Lonjezano. Mwaiwo udapatsidwa cabe kwa ana ao. (Numeri 14:10-12). Ngakhale Mose yemwe adaletsedwa kulowamo. Ngakhale anali wamkuro koposa koma adalephera pamodzi. Anthu anali kudandaula cifukwa cakuzowa madzi. Polema ndi kusakhulupirira kwao iye anaonetsa ukali ndi kuwapsera mtima. Iye anasowa kupirira kwa kuti apitilirebe. (Numeri 20:10-12). Inali nthawi ya kuti munthu wina atenge ncito yobvutayi ya kutsogolera ana ao kunka mu Dziko Lalonjezano.

Ici cidacitikaci ndi phunziro lalikuru kwa ife tonse. Anthu akuru koposa amagwa. Ngakhale tiyang'ane kwa iwo motani kukhala citsanzo cathu tiyenera kukumbukira kuti kuli cabe mmodzi yekha amene ali citsanzo copanda banga, Yesu Kristu. Ikani maso anu pa Iye. Mlembi wolembera kwa Ahebri atikakamiza ife kuti 'tithamange mwa cipiriro makaniwo adatiikira, ndikupenyerera woyambira ndi womariza wa cikhulupiriro cathu.' (Ahebri 12:1-2).

Yoswa adaphunzira za mbiri kucokera kwa Mose koma anaphunzira kumayang'ana koposa anthu. Iye anakhala wolimba mu cikhulupiriro, cikhulupiriro ca iye mwini. Iye adayesedwa ndipo anapambana mayeserowo. Wokhulupirika ngakhale pafupi imfa, iye analandira mphotho yace. Iye yekha ndi Kalebi ndiwo awiri omwe adacoka mu dziko la Aigupto, ndiwo analoledwa kulowa mu



Nthawi zina anali kumva ngati Mulungu adamsiya ndipo anali kutaya mtima. (Yeremia 20:7).

Iye sanaloledwa kukhala ndi kazi ndi banja kuti adzimulimbikitsa ndi kumsangalatsa. (Yeremiya 16:1).

Yeremiya sanali munthu yemwe tikadamsankhira cinchito cobvuta cotereci. Tingaganzire za iye kuti anali wofooka. Iye aoneka kuti ngati anali penatu munthu wosakondwerera, munthu wansangala yemwe tonsefe tingamukonde.

Komabe ngakhale zinali zotere Mulungu anadziwa munthu yemwe anali kumufuna. Iyetu safuna 'kanthu kopangidwa kale'. Amuna omwe anapatsidwa mphatso, olimba ndi okhoza kudzimenyera okha kawirikawiri samamvera kuti amasowa Mulungu. Iwo nthawi zambiri amanyengedwa pomakhulupirira mu mphamvu za iwo eni. Mulungu amafuna anthu omwe saoneka monga kanthu kuti akhoza kuwapanza ndi kuwaumba monga momwe afunira iye mwini. Izi zidaonetsedwa mwa Yeremiya mu njira yozizwitsa kwambiri. (Yeremiya 18:1-6). Ifetu ndife cabe. Mulungu ndiye amatiumba kukhala cotengera comwe angacigwiritse nchito. Nthawi zina timayimba:

"Khalani ndi njira zanuzanu Ambuye,
Khalani ndi njira zano.
Inu ndiye woumba, Ine ndine dongo.
Ndiumbeni ndi kundipanga,
Monga mwa cifuniro canu
Pamene ine ndiri kulindira
Modzipereka ndi wa bata."

Jese, atate wace wa Davide, anaphunzira phunziro limodzimodzi. Samueli, mneneri, anadza kumudzi wace kufunafuna munthu kuti m'amudzoze kukhala mfumu m'malo mwa mfumu Sauli. Iye anadziwa kuti ayenera kukhala mmodzi wa ana a Jese. Ndipo pamene anafunsa kuti awaone ana ace anali okhawo omwe anali ndi 'maonekedwe abwino' anadza ndi Jese, ao anthu anali kuwanyadira ndi kuwayamikira.

mbali ya nzeru yace. Mfumu ya Aperezi, Koresi, Ngakhale anali munthu wakunja, anagwiritsidwa nchito mu nzeru ya Mulungu. Tiphunzira mu Yesaya 45:1-4 kuti pamene anamenya nkhondo zace, Mulungu anamgwiritsa nchito kulanga mitundu yocimwa ndi kubwezera mtendere wa Israyeli.

M'buku la Yeremiya, ngakhale sinali tero, anali Israyeli yemwe anali kulangidwa cifukwa ca macimo ace. Mulungu anali kugwiritsa nchito mafumu acikunja kuti acite cilangoci. (Yeremiya 1:14-16).

Yeremiya anapatsidwa cinchito colimbaci cakuuza mtundu wonse wa anthu kuti Mulungu adzawaweruza iwo. (Yeremiya 1:9-10).

2. MUNTHU YEMWE MULUNGU ADAMUITANA

Mungaganizire kuti Mulungu akadaitana munthu wolimba, munthu wouma kuti adzacite nchito yotereyi, Munthu yemwe anaicitapo nchito yonga imeneyi ndi wosacita mantha mnsanga, msilikari kapena. Iyeyutu anali kunka kukaima mwa iye yekha kutsutsana ndi anthu oipa omwe sadzaulandira uthenga wace.(Yeramiya 11:18-19,21; 18:18 ndi 20:2).

Tiphunzira kuti anali mnyamata wamng'ono. (Yeremiya 1:6).

Vesi lomwelinso litiuza kuti anali wosadziwa kulankhula bwino.

Vesi 8 lionetsa kuti anali ndi mantha.

Vesi 17 anacita mantha pa zomwe Mulungu adamuitana kuti akacite.

Nthawi zambiri anali kugwa mphwayi mu nchito yace ngakhale kumaganiza kuti kunali bwino kuti sadabadwa iye. (Yeramiya 20:14-15, 18).



dziko la Kanani. (Numeri 14:30). Mwa awiriwa, Yoswa anapatsidwa mwai waukuru koposa. Iye anali mtsogoleri-wa ao onse amene anabadwira m'cipululu kunka ku dziko lomwe linali colowa ca atate wao. Tiwerenga m'Numeri 27:18-23 kuti kulingana ndi malangizo a Mulungu, Mose adaika manja pa Yoswa namuika iye kukhala wolowa m'malo mwace. Onanitu kuti vesi 18 likuti Yoswa mwa iye munali mzimu asadaikedwe manja. Yoswa anakhala mtsogoleri wa mkuru cifukwa iye anali wokonzekeratu bwino lomwe kupyolera mu zomwe adaziona ndi kucita, mu mtima mwace ndi zonse zomwe zidacitika m'ncito ya Mulungu.

MAFUNSO:

1. Kodi ndingaphunzirenji kupyolera mwa Akristu ena?

2. Kodi mpingo wanga ukadakhala mpingo wotani ngati munthu aliyense wa mu mpingomo akadakhala monga ine ndiliri?

3. Kodi ndi mu njira ziti momwe ife tiliri monga azondi aja omwe adalephera?

MUTU 6

## KUITANIDWA KWA ELISA NDI MULUNGU

LEMBA: 1 Mafumu 19:19-21.
2 Mafumu 2: 1-15.

VESI LOLOWEZA: *"Pamenepo anatola copfunda cace ca Eliya cidamtayikaco.." 2 Mafumu 2:13.*

Nthawi ndi nthawi Mulungu amapereka atsogoleri amphamvu ku mpingo wace, koma monga anthu ena atsogoleriwa amamwalira. Munthu wina amafunika kupitiriza kucoka paja adalekezera iwo; Elisha adaitanidwa ndi Mulungu 'kudzabvala copfunda' ca munthu wamphamvu koposa iye.

1. MULUNGU ADAITANA ELISA KUTI ASINTHE NCITO YACE

1 Mafumu 19:19 atiuza kuti Elisa anali mwana wa mlimi Dzina la atate wace anali Safati ndipo aoneka kuti penatu iyeyu anali mlimi wa cuma. Iye anali nazo ng'ombe zambiri zomwe zinali kulima m'munda mwace.

Elisa anali kugwira ncito ya atate wace ndipotu tsiku lina mundawo ukada dzakhala wace. Palibe kukaika kuti iyeyu anali kuyang'anira tsikulo lomwe adzakhala mlimi wa cuma yemwe anthu ena adzampatsa ulemu.

Ndipo tsiku lina pamene anali kulima m'munda Eliya adampitirira iye pomwe anali kulimapo. Iyeyu anali mneneri wa mkuru. Iyeyu adalankhula ndi mfumu ya kunja motsutsana naye. Ndipo adaitana anthu ace kuti acoke ku cipembedzo ca cikunja conama ndi kusiya zonse za cikunja. Ulaliki wacetu unali wa ukuru ndi wamphamvu kotero kuti anthu ambiri anatembenukira kwa Mulungu.

Komatu Eliya adadziwa kuti anali kumayandikira ku mapeto kwa ncito ya moyo wace.



MUTU 8

## KUITANIDWA KWA YEREMIYA NDI MULUNGU

LEMBA: Yeremiya 1:1-10.

VESI LOLOWEZA: *"Usaope nkhope zao; cifukwa Ine ndiri ndi iwe kuti ndikulanditse iwe, ati Yehova." Yeremiya 1:8.*

Nthawi zina Mulungu amaoneka kuti amaitana munthu yemwe sali woyenera kucita nchitoyo, komatu Mulungu amadziwa zomwe ali kucita. Njira zace siziri njira zathu.

> *"Pakuti maganizo anga sali maganizo anu, ngakhale njira zanu zisiri njira zanga, ati Yehova. Oakuti monga kumwamba kuli kutari ndi dziko lapansi, momwemo njira zanga ziri zazitari kupambana njira zanu, ndi maganizo anga kupambaba maganizo anu." (Yesaya 55:8-9).*

Kuitanidwa kwa Yeremiya kunali citsanzo ca zimenezi.

1. KUBVUTA KWACE KWA CINCHITO

Mbali ya kumaiko aku M'mawa wapakati, komwe kuli kumalo komwe Yeremiya anabadwira, ndi pakatikati pa nkhondo kulimbana kwambiri. Ayuda ndi a Arab aukirana wina ndi mnzace. Yerusalemu wazunguliridwa ndi mitundu ya anthu omwe ali aukali. Ngakhale Yeremiya Anabadwa zaka 2600 zapitazo zinthu sizinali zositha kwenikweni monga ziliri ai. Mitundu yonse yozungulira Yerusalemu m'malo mwakuti ikadakhala yogwirizana pa kulimbana kwao ndi Israyeli inali kulimbana yokha wina ndi mnzace. Ndipo pamene anali kumenyana, Yuda, (mbali ya kummwera kwa ufumu wogawikana wa Israyeli) mbali ya pakati pa kummawa, anaponderezedwa nawo pamodzi.

Buku Lopatulika limaphunzitsa kuti ngakhale ndi anthu omwe amayambitsa nkhondo Mulungu nthawi zina amawagwiritsa nchito monga

ndicite ciani?" Ndipo pakumva kupfuula kwace kwa kusowa Yesu anatenga cikho cace cija, namwa zonse zonyansa ndi zace zinalimo zija kufikira cinali copanda kanthu mkati mwace, ndipono anadzazamo ndi madzi a moyo. Yesu anapita pa Mtanda kukamwa cikho ca ucimo wathu, kotero kuti tikhoza kulandira moyo watsopano kucokera kwa Iye.

4. OCIMWA OMWE ANAKHULULUKIDWA AMAKHALA ALALIKI OPAMBANA KOPOSA KWA OCIMWA ENA

Yesaya anaona angelo ambiri ozungulira mpando wa cifumu wa Mulungu. Angelo omwe ana-libe ucimo, angelo omwe anali alaliki odabwi-tsa kwambiri. Mulungu anali nao atumiki onsewa okonzekera kuti acite cifuniro cace, koma anaitana nanena kuti "Ndidzamtumiza yani, ndipo ndani adzatimukira ife?" (vesi 8). Mulungu anafuna mthenga kuti apite ndi kuka-nena kwa anthu ocimwa a Israyeli. Iyetu aka-datuma angelo koma afuna anthu odzipereka okha pakati pa anthu. Ndi omwe adaona mfumu, anthu omwe iwo eni adakululukidwa. Mulungu afuna kuuza ena za kukhululukira kwace kwa anthu ocimwa. Ifetu timanena bwino lomwe zinthu zomwe zidacitika kwa ife.

Yesaya sadakakamizidwekonse ai. Iye ana-dzipereka yekha, "Ndine pano! munditumize ine."

Ndi cinthu codabwitsa kotani pamene mwa-muna kapena mkazi akhuzidwa kotero ndi zomwe Mulungu wawacitira kotero kuti iwo ali ololа kutumikira Mulungu mu njira yomwe iye afuna kuti amutumikirire. Mulungu amakonda anthu odzipereka okha.

MAKUNSO:

1. Kodi cosowa cacikuru kwambiri nciani kwa anthu komwe ndikhalako ine?
2. Mulungu nthawi zonse ali kuitana anchito ena oonjezerapo. Kodi ine ndingadzipe-reke ndekha kucitira ciani Mulungu?



Ndipo cotero pomwe anapitirira pomwe Elisa anali kulima, anatenga copfunda cace naciponya pa phewa lace la Elisa. Cinali copfunda pena-tu monga copfunda cofiira comwe a Bantu a ku Transkei amabvala kapena comwe Angoni aku Cigawo Cakummawa amabvala. Eliya sadanena liu liri lonse koma Elisa anadziwa comwe izi zida-tanthauza. Uwutu unali mwambo wakuti pamene mphunzitsi ali pafupi kumwalira anali kumapa-tsa copfunda cace kwa wophunzira wace wopa-mbana ena onse. Poteropo anali kuonetsera kuti ndiye amene adzatenga malo ace.

Anthu ena amasankha ncito zao, koma ena amapeza kuti 'awasankhira kale ncito.' Penatu Elisa akadafuna kukhala mlimi wamkuru, koma Mulungu anali ndi nzeru yina. Ngakhale zinali tero, kuti Mulungu adaonetsera poyera cifuniro cace sadam'kakamiza Elisa kuti atenge ncito ya uneneri. Iye anali womasuka kumvera kapena kusamvera. Ndipo Elisa anapempha kuti akala-wire kwa makolo ace makolo ace asadamtsatire Eliya. (1 Mafumu 19:20). Ndipo Eliya adamu-uza kuti anali womasuka kucita monga adafunira, (vesi 21). Elisa adadziwa kuti, ngati Mulungu adamuitana kuti akacite ncito yina iye saka-datha kucita ncito yina mokondwera. Ndipo cotero iye adasiya ncito yace ya kale ndipo anatsimikiza kuti sadzayesedwanso kuti abwere rere kuti adzacite ncito yace ya kaleyi pa-kupha ng'ombe zace zonse zija. (vesi 21). Ndipo myama ya ng'ombe ija anacitira phwando lolawirana ndi abwenzi ace ndipo pomwe anatsa-tira mtumiki wa Mulungu. Iyetu adatenga ci-khasu ca tsopano. Iyeyu anali kumuka kuka-gwira ncito ya kukolola mwa mzimu minda yace. Yesu sakadatha kutsimikiza mau ace akuti "Palibe munthu wakugwira cikasu, nayang'ana za kumbuyo, ayenera Ufumu wa Mulungu." (Luka 9:62).

Ifetu anthu amuno mu Africa tinali nao atsogoleri a uzimu abwino koposa. Anthu monga David Livingstone ali amodzi a anthu akuru omveka kwambiri omwe anakhala kudziko lino. Iwowa adayambira ncito ya Mulungu m'dziko lathu lino, koma ena adayenera kutsatirapo

ngati ncitoyi idati ipitirire. Sionsewatu omwe anali omveka iai, komabemphata uja unazazidwa. Mulungu wapatsa atsogoleri, osati pakati pa a mishonare okha iai, komansotu atsogoleri ena a cikuda. A maritiri aku Kenya ndi ku Uganda ali amodzi a Akristu omveka kwambiri omwe adziwidwa m'dziko lapansi. Komatu atsogoleri a dziko lapansi anapita (amafa). Tsikutu la atsogoleri a cimishonare liri pafupi kuti adzapite. Mulungu ali kufuna amuna ena atsopano kuti adzaze mphatawo. Kodi uli wolola kuti copfunda ciponyeredwe kwa iweyo?

2. ELISA ADAPHUNZIRA NCITOYI KUCOKERA KWA MUNTHU YEMWE ADAIDZIWA KOPOSA

Pamene Mulungu aitana munthu kukhala mlaliki kapena mtsogoleri wa Cikristu wa mtundu wina amafunatu kuti iye aphunzitsidwe kuti akhale mtsogoleri wa bwino. Siciri cokwanira kungoitanidwa kokha ai. Ife tifunikatu kuwaphunzira Mau a Mulungu kuti tiwadziwe bwino. Ife tifunika kuphunzira momwe tingafikire kwa anthu ena kuti adze kwa Kristu. Mlaliki pena m'phunzitsi nthawi zonse amakhala wopambana pophunzira kucoka kwa munthu wina yemwe ali wodziwa koposa iye mwini. Paulo adauza mlaliki wa cinyamata, Timoteo, "Ucite cangu kudzionetsera kwa Mulungu wobvomereseka, wanchito wopanda cifukwa cakucitira manyazi, wolunjika nao bwino mau a coonadi." (2 Timoteo 2:15).

Eliya adadziwa kufunika kwace kwa kuphunzitsira ena kuti acite nchito ya Mulungu. M'mshiku amene aja maskulu a aneneri anali ambiri. (2 Mufumu 2:3,4,7). Elisa anadziwa kufunika kwace kwa kuphunzira kucokera kwa munthu wonga Eliyayu. Iye adamtsatira nthawi zonse pafupipafupi naphunzira nchitoyi kucokera kwa iye. Ndithudi iye adaumirira kumakhaladi cifupi ndi Eliya kufikira kucimaliziro. (2 Mafumu 2:2,4,6).

Kodi ife tiri olola kupereka nthawi ndi ndarama kuti tiphunzire, kuti tikhale ofunikira



mphamvu ya Mulungu yomuzungulira iye. (Yesaya 6:4). Palibe munthu yemwe angafike cifupifupi ndi Mulungu cotere nkupanda kuona kuti ali wocepa ndi wosayera. Ngati tiri ndi maganizo a akuru a ife eni cifukwa ca kuti ifeyo tiri ndi maganizo ocepa Kwambiri a Mulungu. Ngati timva kuti tiri anthu abwino ndi cifukwa cakuti sitinaone kuyera kwace kwa Mulungu. Pamene Yesaya anaona kuyera kwace kwa Mulungu iye anapfuula ndikuti, "Tsoka kwa ine! Cifukwa ndathedwa; cifukwa ndiri munthu wa milomo yonyansa; cifukwa kuti maso anga aona Mfumu, Yehova wa makamu." (Yesaya 6:5).

Mulungu sangagwiritse munthu kufikira munthu uja atadziona kucimwa kwace ndi kupanda mtengo kwace komwe iye aliri. Mulungu amtionetsera ife kucimwa kwathu kutitsogolera. Amatitsogolera kukulapa kuti tikayeretsedwe kuticotsera macimo athu. Yesaya anadziona yekha kuti anali wotayika kuti "anapezedwa." Kulapa kwace kunali tanthauzo la kukhululukidwa. Tiwerenga kuti, "Pompo anaulukira kwa ine mmodzi wa aserafi, ali nalo khala lomoto m'dzanja mwace, limene analicotsa ndi mbaniro pa guwa lansembe; nakhudza balo kukamwa kwanga nati, Taona ici cakhudza milomo yako; ndipo mphulupulu zako zacotsedwa, zocimwa zako zaomboledwa." (Yesaya 6:6-7).

Kuli nthano ya munthu wina wa ci African yemwe analota maloto. Iyeyu anadziona yekha kuti anakhala pa kuzungulira gome lalikuru ndi anthu ena. Ndipo Yesu anali kuyenda kuzungulira gome lija ndi mphika wa ukuru. Mu mphikamo munali 'madzi a moyo' ndipo pamene anafika pa munthu aliyense anawatsirira m'cikho ca wina aliyenseyo. Ndipo pomwe adafika kwa wolotayo anawerema capaphewa pace ngati afuna kumutsirira koma sadamutsiriramo ai anapitirira. "Ambuye," anapfuula munthu uja, "Ndifuna madzi a moyo." Ndipo Yesu analoza mu cikho cace. Ndipo pomwe iye anayangana m'cikhomo anaona kuti munadzala kale ndi zinthu zonyansa, za dothe,zinthu zokwawa pansi pansi. "Koma Ambuye," anapfuula "Nanga

kukondwerera ndi zipatso za kupambana ndi masiku a cuma a lerowa? Kodi ine ndiri kudera nkhawa kapena ndiri kucita monga momwe ena ali kucitira?

2. PA NTHAWI YAKUSOWA KWACE ANATEMBENUKIRA KWA MULUNGU

Pakugwiridwa ndi mzimu mu nthawi ya byuto lomwe linali ku mtundu wonse Yesaya anacita cinthu comwe Mkristu wina ali yense akadacita pa nthawi yoteroyo, iye anatembenukira kwa Mulungu. Iye analowa m'nyumba ya Mulungu kukapemphera. (Yesaya 6:1). Ananyamula maso ace, m'masomphenya anaona ulemerero wa a Ambuye. Mfumu wa dziko lapansi adafa koma Mfumu wa Mafumu analibe wa moyo pa mpando wace wa cifumu wa dziko lonse. Mfumu wa dziko lapansi adalephera koma mfumu wakumwamba anali wa ulemerero kuona ndi wangwiro mu njira zace zonse. Yesaya adaona Mulungu atazunguliridwa ndi angelo ocedwa aserafi, omwe anatumikira msana ndi usiku. (vesi 2). Nthawi zonse anali kuimba za kuyera kwace ndi ulemerero wace. (vesi 3).

Ndi cinthu codabwitsa kudziwa kuti pa cobvuta coopsa conse comwe cimacitika pa dziko lapansi lino, ngakhale atsogoleri a dziko lino alephera Mulungu ndiye ali wolamulirabe. Iye salephera konse. Monga momwe kanyimbo ka ana kanena kuti:

"Mulungu ali pa mpando wace wa ufumu,
Ndipo iye adzakumbukira ace omwe
Mwa mayesero adzatikakamiza ife
Ndi katundu kutikhumidwitsa,
Iye sadzatisiya ife tokha."

Pamene zinthu zaipa osayang'ana pansi koma m'mwamba.

3. ULEMERERO WA MULUNGU UDAMPANGITSA KUDZIONA KUTI ANALI WOSAYENERA

Zomwetu zidaoneka kwa Yesaya za Mulungu ndi kuyera kwace zinalidi zoona. Iye anamva



kwambiri kwa Mulungu? Kodi tiri olola kuti tipite ku seminare ngati Mulungu afuna kuti titero? Kodi tiri olola kuti tiphunzire kucokera kwa atsogoleri athu a uzimu? Wacikristu mu Zambia udzaima kapena udzagwa malinga ndi momwe atsogoleri ace aliri.

3. ELISA ANAFUNITSA KUKHALA WOPAMBANA WENIWENI WA MULUNGU MONGA AKADATHERA

Elisa anakhalitsa cifupi ndithu ndi mtsogoleri wace wa dziko lapansi kuti asapitidwa kanthu Kena kali konse ai. Kafikira kumapeto kwa moyo wa Eliya tipeza Elisa ali kufunafuna kulandira dalitso loposa. Mu 2 Mafumu 2:9 tiwerenga:

> *"Ndipo kunali ataoloka, Eliya anati kwa Elisa, Tapempha cimene ndikucitire ndisanacotsedwe kwa iwe. Ndipo Elsa anati, Mundipatse magawo awiri a mzimu wanu akhale pa ine."*

Pamene bambo wa pa banja amwalira muno mu Zambia mwana woyamba wa mwamuna ndiye amatenga mwai waukuru woposa ena. Elisa anali kupempha colowa ca mwana woyamba. Pakati pa'ana a aneneri onse. Elisa yekha ndiye anali cifupifupi kwambiri ndi Eliya ndipo iye anafuna kuti alandire copambana koposa comwe Eliya angapereke. Iye anafuna kugawana naye kanthu kena ka mphamvu ya uzimu yomwe adaiona mwa Eliya Ndipo Eliya adamuuza kuti adapempha cinthu colimba kwambiri. (vesi 10). Ndi cinthu cabwino kupempha zinthu zazikuru za Mulungu. William Carey m'mishonare wamkuru wa Baptist yemwe adapita ku dziko la India anati, "Yembekezerani zinthu zazikuru kocokera kwa Mulungu, yesani kucitira zinthu zazikuru Mulungu."

Eliya sadafe ai. Iye anatengedwa kunka kwa Mulungu ndi akavalo a moto. (vesi 11). Mulungu adapereka mwai wapadera kwa mtumiki wace wokhulupirika. Kodi cinthuci cidaonetsera bwanji nanga kupambana kwace kwa zinthu kwa munthuyu Elisa. Iyeyutu adamsowa muntha

wamkuruyu kwambiri. (vesi 12). Komatu iyeyu sadangoima kumalira ai. Iye anatenga copfunda ca Eliya nayamba kucita zinthu zazikuru zomwe Eliya anali kucita. (vesi 13-14). Eliyatu adapita loma Mulungu anali cimodzimodzi. Comwe akhoza kucita ndi munthu wina akhoza kucitanso ndi munthu wina. Pamene mzimu wa Mulungu akhala pa munthu anthu ena amauona. (vesi 15). Paulo adati kwa Timoteo, "Ndipo zimene wazimva kwa ine mwa mboni zambiri, zomwezi uikize kwa anthu okhulupirika,amene adzadziwa kuphunzitsa enanso." (2 Timoteo 2:2). Iye amene adaphunzira kucokera kwa mnzace iyeyunso adakhala mphunzitsi. Umutu ndimo momwe nchito ya Mulungu imatengedwera kucoka kwa mbadwo umodzi kufikira wina.

MAFUNSO:

1. Cifukwa ciani mipingo imafuna anthu ophunzitsidwa?
2. Kodi ndingatani kuti mpingo wanga ukhale ndi munthu yemwe ali mtsogoleri adaphunzitsidwa?
3. Kodi ndiri kucita ubwino wanga wonse kudzionetsera monga wanchito wobvomerezeka ndi Mulungu?



MUTU 7

## KUITANIDWA KWA YESAYA NDI MULUNGU

LEMBA: Yesaya 6:1-8.

VESI LOLOWEZA: *"Ndipo ndinamva mau a Ambuye akuti, Ndidzatumiza yani, ndipo ndani ndzatitumikira ife? Ndipo ine ndinati, Ndine pano; munditumize."*
*Yesaya 6:8.*

Kwa anthu ena kuitana kwa Mulungu kumadza m'Njira yosayembekezeka pa nthawi yomwe pali kubvutika pakwambiri. Yesaya anali mmodzi wa anthu oterewa.

1. INALI NTHAWI YAKUSOWA KWAKUKURU KWA MTUNDU WONSE

Yesaya anali kukhala mu ufumu wa Yuda, mbali ya m'mwera ya mtundu wogawikana wa I Israyeli. Kwa zaka makumi asanu Yuda analamuliridwa ndi mfumu imodzi, Uziya. Iyeyu anali mfumu yabwino, wokondwedwa ndi anthu. Mu nthawi ya ulamuliro wace yonse anthu anakondwera ndi mtendere woposa womwe anali nao pa masiku a Solomo ndi Davide. Koma mu nthawi yao ya ulemerero ndi cuma anthu anayamba kutembenuka kucoka kwa Mulungu. Usiya mwini anacita ucimo woopsa kwakukuru. (2 Mbiri 26:16). Ndipo Mulungu anamlanga iye cifukwa ca ucimo wacewo. (Mbiri 26:17-21). Komabe ngakhale zinali tero kugwa kwace ndi imfa yace inakhala nthawi yaikuru ya maliro mu mtundu wonsewo.

Inali nthawi ya kufa kwace kwa Uziya pamene Yesaya anaitanidwa kukhala mneneri. Iyeyu anamkonda kwambiri mfumu uja ndipo anagwetsedwa mphwayi kwambiri ndi kulephera ndi imfa ya mfumuyi. Iyeyu anagwetsedwa mphwayinso cifukwa ca macimo a anthu.

Kodi anthu a mu dziko lathu ali kuyamba kumatembenuka kucoka kwa Mulungu pamene ali